


# *Nodi Mzimu Woyera*

## *Ndi Chiyani?*

 . . . movutirapo kwa msonkhano. Msonkhano uno ndi woti ukhale msonkhano wosiyana pang'onopo kuposa umene ife timakhala nawo nthawizonse pano. Mochuluka, nthawi iliyonse pamene ife tibwera palimodzi pano, ndi msonkhano kwa . . . wa kuchiritsa kwa odwala ndi wa zosowa za mthupi. Ndiko kutsimikizira kumene kumayikidwa pa izo. Koma usikuuno ife tayamba chitsitsimutso ichi chifukwa cha kuchiritsa kwa solo, m—mzimu wa munthu.

Komabe, Ambuye akalola, Lamlungu mmawa, pa Sande sukulu, Lamlungu mmawa, ife tikuti tidzakhale ndi kupempherera odwala ndi mzere wachizolowezi wa machiritso, wa Lamlungu mmawa, Ambuye akalola. Ndipo mausiku a sabata awa, ife tiri opsyinjika kwakukulu kuti tiyankhule pa zinthu Zamuyaya za—solo.

<sup>2</sup> Tsopano, ife tikudziwa kuti pamene—thupi liri lochiritsidwa, izo zimatipanga ife tonse kukondwa, chifukwa ife timadziwa kuti izo motsimikiza zimasonyeza kuti Mulungu wathu amachiza odwala. Koma munthu wodwala ameneyo, ngati iwo akhala moyo motalika kokwanira, mwinamwake adzakhala atadwala kachiwiri, mwinamwake ndi matenda omwewo omwe iwo anachizidwa kwa iwo, ndipo chimenecho sichimachotsa machiritsowo. Adokotala akanati apereke mankhwala a chibayo, ndipo mwinamwake masiku awiri otsatira iwo akanati afe ndi chibayo iye atawauza kale iwo kuti achira. Ichu chimayambira kachiwiri. Koma pamene solo imeneyo yachiritsidwa, iwe umakhala nawo ndiye, mwa iwe, Moyo Wamuyaya.

<sup>3</sup> Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ife tiri pafupi kwambiri ku Kudza kwa Ambuye Yesu, mwakuti icho chikutikakamiza ife kuti tizichita zonse zimene ife mwakukhoza tingakhoze kuti tiibweretse solo iliyonse ku Ufumu, ndi kuti tibweretse Ufumu kwa anthu, kuti ife tikhoze kukhala ochiritsidwa mu mizimu yathu. Ine ndikukhulupirira kuti thupi la Yesu ndilo thupi lodwalitsitsa limene ine ndikulidziwa; ilo ndilo, t—thupi, thupi lauzimu la Khristu pa dziko lapansi, ndi lodwalitsitsa.

<sup>4</sup> Ndipo tsopano, ife sitiri kulinga za kukusungani inu motalika kwambiri pa usiku, chifukwa pa usiku woyamba ife tiribe malo kuti tiwakhazike abwenzi athu okondedwa. Ife tiri mu ntchito ya kumanga tchalitchi chatsopano, kachisi wamkulu pomwe pano pa malo awa, kapena kulikonse kumene Ambuye ati atitsogolere; koma momwe ife tikudziwira, ndi pano.

<sup>5</sup> Ndipo tsopano ife tapereka kwa msonkhano, Lachitatu mpaka Lamlungu. Koma ndiye Lamlungu, ndi kutsekera kuti tilowe mu tchuthi cha Khrisimasi, koma izo . . . pamene Ambuye ati atiwuze ife kuti tiyimire, imeneyo idzakhala nthawi yake. Ife sitikudziwa basi chomwe zotsatira zake ziti zidzakhale. Koma tikukhulupirira kuti anthu pano pa kachisi ndi mipingo yapaulongo yathu, yomwe ili, umodzi wa iwo ndi—ndi kachisi wa chiyero ku Utica, amene M'bale Graham Snelling ali m'busa, ndi mu New Albany kumene M'bale—M'bale Junie Jackson ali m'busa, ndiponso kunjwa uko pa msewuwaukulu kumene M'bale Ruddell ali m'busa. Ife ndi iwo tiri, mipingo yapaulongo kwa kachisi uyu, ife tikuyesera kuti tiwabweretse—anthu athu alowe mu chiyanjano chabwinoko ndi Khristu. Ndicho cholinga chathu. Chotero ine ndasankha kuti ndiwerenge ndi kuti ndiphunzitsebe, kwa mausiku ena angapo . . .

<sup>6</sup> Usikuuno ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa phunziro la: *Kodi Mzimu Woyera Ndi Chiyani?* Ndipo mawa usiku, ine ndikufuna kuti ndidzalalikire pa: *Kodi Iwo Unaperekedwera Chiyani?* Ndipo Lachisanu usiku . . . Ndipo, kwa ojambula, ine sindikufuna izi zidzajambulidwe Lachisanu usiku: *Kodi Ine Ndingalandire Motani Mzimu Woyera?* ndipo *Ndingadziwe Motani Pamene Ine Ndiri Nawo Iwo?* Ndiyeno ife tidzangolola, ndiye nkuwona chimene Ambuye ati adzatitsogolere ife, kwa Loweruka ndi Lamlungu. Ndipo Lamlungu mmawa, msonkhano wamachiritso, ndi msonkhano wina wa ulaliki wa Lamlungu usiku.

<sup>7</sup> Ndipo tsopano ife tikufuna aliyense kuti adziwe zimenezo . . . Ndipo ine ndikudziwa zojambulira zikuzungulira mu chipinda chakumbuyo, ndipo ife ndikukhumba kuti ndinene ichi. Chifukwa, mu misonkhano iyi monga uwu, ya mtundu waulaliki, ife timakhala ndi anthu ochokera ku chipembedzo chosiyana cha mipingo omwe aphunzitsidwa mu dera lawo lawo la kakhulupiridwe, mmodzi aliyense. Ndipo izo zonse nzabwino. Ine sindinayambe ndafunapo kukhala wolakwa pa kufetsa kusagwirizana pakati pa abale. Ndipo kunjwa mu misonkhano, ine ndimangolalikira pa Zoonadi zazikulu za ulaliki wa Lemba, pa zomwe abale omwe amathandizira msonkhano wanga amakhulupiriramo. Koma, mu kachisi kuno, ine—ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa zomwe ife timakhulupirira. Chotero, ngati inu—ngati inu simuli kuzimvetsa izo, ine ndikanakhala wokondwa kwambiri kuti ndilandire kalata yaing'ono kapena cholembedwa kuchokera kwa inu, kuti mundifunse ine funso la—la chifukwa chomwe ife timakhulupirira izo moteromo. Ndipo ine ndikanakhala wokondwa kuti ndiyese kuzifotokoza izo mwakukhoza komwe ine ndingakhoze.

<sup>8</sup> Inu mukudziwa, mpingo uliwonse, ngati inu mulibe chiphunzitso, sindinu mpingo ayi. Inu muyenera kuti mukhale ndi chinachake chimene inu mumachiyimira, mfundo zina

zomwe inu muli kugwirirako. Ndipo mosasamala za chomwe munthuyo amayanjana nacho kapena chipembedzo chake chingakhoze kukhala, ngati munthu ameneyo ali wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu, ameneyo ndi m'bale wanga kapena mlongo wanga, mosasamala za... Ife tikhoza kusiyana mu zinthu zina, monga kutalikirana kwa kummawa ndi kumadzulo, koma ife tikadali abale. Ndipo ine sindikanati ndichite kalikonse koma kuyesa kuti ndimuthandize m'bale ameneyo kuti aziyenda mofupikira, kuyenda kwabwino kupita kwa Khristu. Ndipo ine ndikukhulupirira Mkhristu aliyense weniweni, woona akanachita chinthu chomwecho kwa ine.

<sup>9</sup> Tsopano, ine ndafunsa kachisi uyu... Tsopano, ife sitiri kulowa mu izi mwa msonkhano wankhoka chabe. Ine ndikufuna kuti ndilowe mu izi, ndipo ine ndikufuna inu, ndipo ndakupemphani inu, kuti muwotche mlatho uliwonse umene uli kumbuyo kwanu, ndi kukonza tchimo lirilonse, kuti ife tikubwera mu ichi ndi zonse zomwe ziri mu mitima yathu ndi miyoyo. Ife tiyenera kubwera muno mwa cholinga chokhacho cha kuifikitsa miyoyo yathu mokonzekera Kudza kwa Ambuye, ndipo mosakhala kwa cholinga china. Ndipo monga ine ndayankhula ndi kunena, kuti mwinamwake nthawi yina ine mwina ndingaphunzitse kapena kunena chinachake chomwe chingakhale chosiyana pang'ono ku chomwe winawake, momwe iwo ankakhulupirira icho. Ine—ine ndinachita—sikuti ndabwerera mtsutsano, inu mukuona, ine—ine ndabwera... Ife tiri pano kuti tikonzekere Kudza kwa Ambuye. Ndipo ine ndikuganiza kuti gulu laling'ono ili... .

<sup>10</sup> Ine ndiri nawo abale odzacheza ena ndi ine pano omwe ine ndikuwadziwa, ochokera ku malo osiyana, ndipo ndife okondwa kukhala tiri nawo. Ndipo mosakaika koma chimene mwa omvera akunja uko, alipo ena ochokera kunja kwa mzinda, ochokera kunja kuchokera kozungulira mizinda yathu yaying'ono yolumikizana kuno. Ndipo ife tiri okondwa kukhala tiri nanu, ndi oyamikira kwambiri za inu, ngati inu mumatikonda ife mokwanira bwino kuti mubwere kudzamvera zinthu zimenezi. Mulungu... Mutatengera kwanu limodzi nanu, m'bale wanga, mlongo, chuma cha mtengo kwambiri chomwe Mulungu angakhoze kutsanulira mu mtima wanu, ndilo pemphero langa.

<sup>11</sup> Ndipo kwa kachisi wamng'ono uyu, powona kuti ine ndikukhulupirira kuti ali mmodzi wa anthu abwino kwambiri omwe ine ndikukhulupirira alipo pa dziko lapansi, amapita ku kachisi uyu. Tsopano, ine sindinati konse, “onse” anthu abwino kwambiri. Ine ndinati ena a anthu abwino kwambiri pa dziko lapansi amapita ku kachisi uyu. Koma monga tsiku ndi tsiku, kulowa mobwerera, kuchoka ku msonkhano kumka ku msonkhano, ine ndikuwona kusowa kwakukulu kwa kachisi uyu, kusowa kwakukulu mwa iye, ndipo ndiko

kwa kudzazitsa, kapena kudzipereka, moyo wakuya, kuyenda kofupikirana ndi Mulungu. Ndipo ine ndawalonjeza iwo kuti ndichita ichi, kuti tikhale ndi Uthenga uwu kwa iwo. Ndipo ndife oyamikira kukubweretsani inu mkati mwa kuyanjana ndi ife pozungulira Mawu a Mulungu, pamene ife tikuphunzitsa ndi kuyesa kubweretsa poyera.

<sup>12</sup> Tsopano, mausiku atatu oyamba ife sititi titenge phunziro kuti tilalikirepo, koma Uthenga kuti tiphunzitse kuchokera mu Mawu a Mulungu.

Ndipo tsopano, pakuti, ine sindikanati ndimufunse wina aliyense kuti achite chirichonse chimene ine sindingachichite inemwini. Ndipo sabata ino yakhala Kalvare yathunthu kwa ine. Ine ndakhala pafupi kwambiri ku—ku chidima, monga ine ndikanati ndiyikire izo, mpaka ine ndinali pafupi kusokonezeka. Koma ine ndagonjera kwathunthu chifuniro chirichonse, ndi chirichonse chimene ine ndikuchidziwa, kwa Ambuye.

<sup>13</sup> Usiku wina, cha kuyandikira pang’ono patadutsa pakati pa usiku, mkazanga ndi ine, titatha kukhala, ndi kupemphera ndi kuyankhula kwa Ambuye, pa kampando kakang’ono ka phazi mu . . . chipinda chathu chakukhomo, ndi Mabaibulo awiri otsegula, ife tinadzipereka ifeeni mwatsopano kwa Mulungu, ku utumiki wathunthu, kuti ife tikakhoze kugonjera zifuniro zathu zomwe, ndi chirichonse, ndi lingaliro lililonse lotsutsa, kuti timutumikire Ambuye Yesu.

Ndipo ine ndikudalira kuti icho chakhala chiri cholinga chanu, inunso, kuti inu mwachita chinthu chomwecho. Ndiye pamene ife tiri kubwera usikuuno, ife tiri kubwera pa malo oyera, pakati pa anthu omwe akhala akupemphera, ndi kusala, ndi kupita kukakonza, ndi kukhala akukonzekera kuti alandire chinachake kuchokera kwa Mulungu. Ndipo ine ndikudziwa kuti iye yemwe ati abwera wanjala sati apite kwao wanjala, koma Mulungu amudyetsa ndi Mkate wa Moyo.

<sup>14</sup> Tsopano, tisanati ife tiwerenge kuchokera ku Bukhu Lake lopatulika, tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi chabe kwa pemphero.

<sup>15</sup> Ambuye, kwaperekedwa kale pemphero mu malo ano usikuuno. Pakhala pali . . . nyimbo za Zioni zakhala zitayimbidwa ndi ana Anu. Mitima yawo yakhala itakwezidwera mmwamba. Ndipo ife tabwera muno kuti tidzadzipereke tokha kwa Inu, ndi kuti tidzakupembedzeni Inu kuchokera mu kuya kwa solo yathu. Ndipo ife tikuyitanira izi ku kukumbukira Kwanu, Ambuye, kuti Inu munanena pamene Inu munakhala pamwamba pa phiri ndipo munawaphunzitsa ophunzira Anu, “Odala ali iwo omwe amva njala ndi ludzu la chilungamo, chifukwa iwo adzakhutitsidwa.” Inu munalonjeza izo, Ambuye. Ife tikubwera usikuuno ndi mitima yotseguka.

Ife tikubwera, anjala ndi mwaludzu, ndipo ife tikudziwa Inu musunga lonjezo Lanu.

<sup>16</sup> Pamene ife tikuyesera kuti tisegule masamba opatulika awa a Baibulo, kuti tiwerenge kuchokera mwa Ilo zamkatimo, mulole Mzimu Woyera ungotengera Izo ku mtima uliwonse. Ndipo mulole Mbewu imeneyo igwere pansu kupita mwakuya, chikhulupiriro cholemera chomwe chiti chibweretse lonjezo lililonse limene Mawu apanga. Timvereni ife, Ambuye, ndipo tiyeretseni ife, ndipo tiyeseni ife. Ndipo ngati pati pakhale chinthu chosayera chirichonse chokhudza ife, Ambuye, tchimo lililonse losalapidwa, chirichonse chomwe sichiri chabwino, chiwululeni icho tsopano lino, Ambuye, ife tiyenda molunjika basi ndi kuchichita icho, pakuti ife tikuzindikira kuti ife tikukhala moyo mu mithunzi ya Kudza kwa Ambuye Yesu. Ndipo ife, O Mzimu Woyera, tabwera mu mithunzi ya Chanu—chilungamo Chanu usikuuno, ndipo ife tikuchonderera kudzipereka kwatsopano, ndi kudzipatula, ndi kudzazitsidwa kwa Mzimu Woyera mu miyoyo yathu.

<sup>17</sup> Powona moto wa zitsitsimutso ukuyamba kuthima, tiroleni ife tiponyerepo nkhuni za Mawu, kuti Iwo akakhoze kuyatsa moto watsopano, kuti mitima yathu ikhale ili yodzaza ndi kudzipereka. Tiyeretseni ife, Ambuye, kupyolera mu Mawu Anu ofunika ndi Magazi Anu, ndi chisomo Chanu, ife tikuchonderera. Ndipo mathokozo onse ndi mayamiko akhala ali Anu. Tengani kukondera konse kuchokera mu mitima yathu. Tiyeretseni ife, O Ambuye. Tipatseni ife mitima yangwiro, ndi manja oyera, ndi malingaliro oyera, kuti ife tikakhoze kubwera mu malo Anu opatulika, usiku ndi usiku, tikusangalala ndi kudzazidwa ndi Mzimu Wanu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, ndi chifukwa cha Iye. Amen.

<sup>18</sup> Ine ndikukhumba kuti ndiwerenge Mawu pakali pano. Ndipo pamene... Ine ndikukufunsani inu kuti mubweretse Mabaibulo anu, mapensulo anu, mapepala anu, chifukwa cha Malemba. Ngati inu muli kukhumba kuteru, icho chikhala chabwino kwambiri. Ndipo tsopano pamene inu muli kufika ku mutu wa 7 wa Machitidwe, kuti tiyambire nawo; kuti tiyankhe funso, kapena kuti tiyambe mwa kuyankha funso: *Kodi Mzimu Woyera Ndi Chiyani?*

<sup>19</sup> Palibe kanthu kamene kati kadzamugonjetse Satana, sipanayambe pakhala kalikonse pa dziko lapansi panobe kamene kanakhoza konse kumugonjetsa Satana, monga Mawu a Mulungu. Yesu anawagwiritsa ntchito Iwo mu nkondo Yake yaikulu; Iye anati, “Izo zalembedwa . . .”

<sup>20</sup> Ndipo mmawa uno, pamene ine ndakhala ndikumvetsera, masiku pang’ono apitawo, ku kuwulutsa kumene kumawoneka ngati kukufuna kuti uze kuti chilengedwe chinangochokera ku maphululusa ena ake atapemereredwa palimodzi, ndi fosifeti

wina, ndi mapulusa pang'ono a dziko lapansi, ndipo kufunda kwa kuwala kwa dzuwa kunalenga nyongolosi ya moyo ndipo kunatulutsapo moyo. Ndi zopusa bwanji! Pamene, kuwala kwa dzuwa kukanapha nyongolosi iliyonse ya moyo. Iyikeni nyongolosi mu kuwala kwa dzuwa, iko kungaiphe iyo pomwepo. Ndipo palibe chinthu choterocho; koma Satana amayesera kumenyera chimenecho pa ine. Ndipo ine nditakamutenga Rebekah wanga wamng'ono ku sukulu mmawa uno, ndipo ndiri pa msewu pobwerera, ine ndinayamba kutsegula pa wailesi kachiwiri; ndipo ine ndinaganiza ine ndifika mu zinthu zijazi kachiwiri, kotero ine ndinangopotokolera mmbuyo iyo kuizimitsa.

Ndipo pamene ine ndinali kupita chokwera msewu, Satana anati kwa ine, iye anati, “Kodi iwe ukudziwa kuti Munthu uyu yemwe iwe umamutcha Yesu anali munthu chabe monga, tsiku lina mu tsiku Lake, monga Billy Graham kapena Oral Roberts. Iye anali munthu chabe yemwe anayamba kukhala ndi anthu pang'ono akusonkhana momuzungulira Iye ndi kumanena kuti Iye ndi Munthu wamkulu, ndipo patapita kanthawi Iye anakhala wokulirapo, ndiyeno Iye anakhala mu—mulungu kwa iwo. Ndipo tsopano izo zafala konsekonse mu dziko, chifereni cha Iye, ndipo ndizo zonse.”

<sup>21</sup> Ine ndinaganiza, “Ndiwe wabodza bwanji!” Ndiyeno ine ndinatembenuka basi pamene ine ndinali kuwoloka Msewu wa Graham. Ine ndinati, “Satana, iwe yemwe ukuyankhula kwa chikumbumtima changa, ine ndikanafuna kuti ndikufunse iwe zinthu zingapo. Anali ndani uja yemwe aneneri Achihebri ankamukamba kuti akanati adzabwere? Anali ndani Mesiya wodzozedwayo? Nchiyani chinali pa amuna ajawa omwe ankamuwoneratu Iye ndipo ananena za moyo Wake, zikwi za zaka Iye asanafike kuno? Anali ndani yemwe analosera izo basi mpaka pa lemba? Ndipo pamene Iye anabwera, iwo anati ‘Iye anawerengedwa palimodzi ndi ochimwa,’ ndipo Iye anatero. ‘Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu,’ ndipo iye anatero. ‘Iye anapanga manda ake palimodzi ndi olemera, koma Iye akanati adzawuke, tsiku lachitatu,’ ndipo Iye anatero. Ndiyeno Iye analonjeza Mzimu Woyera, ndipo ine ndiri nawo Iwo. Kotero iwe ukhoza mwina kungochoka kwa Iwo, chifukwa izo zalembedwa mu Mawu, ndipo Mawu aliwonse ali owona.” Ndiye iye anachokapo. Ingompatsani iye Mawu, izo zimachita icho. Iye sangakhoze kupirira nawo Mawu amenewo, pakuti Iwo ali odzozedwa.

Tiyeni tiyambe kuwerenga usikuuno mu mutu wa 7 wa Bukhu la Machitidwe.

*Ndiye mkulu wansembe anati, Kodi zinthu izi ziri chomwecho?*

*Ndipo iye anati, Amuna, ndi abale, ndi atate, mvetserani; Mulungu wa ulemmero anawonekera kwa kholo lathu Abrahamu, pamene iye anali mu Mesopotamia, asanakakhale iye mu Harani,*

*Ndipo anati kwa iye, Tuluka iwe uchoke mu dziko lako, ndi kuchoka kwa abale ako, ndi kubwera ku dziko limene Ine nditi ndidzakusonyeze iwe.*

*Ndiye iye anatuluka kuchokera ku dziko la Akaldia, ndipo anakakhala mu Harani: ndipo kuchokera kumeneko, pamene bambo ake anali atamwalira, iye anamusunthira iye kupita mu dziko ili, limene inu tsopano mukukhalamo.*

*Ndipo iye sanamupatse iye cholowa chirichonse mmenemo, ayi, osati chochuluka monga choti nkupondapo phazi lake: komabe iye analonjeza kuti iye akanati adzalipereke ilo kwa iye ngati lolitenga, ndi kwa mbewu yake yapambuyo pake, pamene apabe iye anali wopanda mwana.*

*. . . Mulungu anayankhula motere, Kuti mbewu yake ikanati idzakayende mu dziko lachirendo; ndipo kuti iwo akanati adzawabweretse iwo mu nsinga, ndi kuwazunza iwo moyipa kwa zaka mazana anayi.*

*Ndipo fuko kumene iwo akanati adzakakhale mu nsinga Ine ndikanati ndidzaliweruze, atero Mulungu: ndipo zitachitika zimenezo iwo akanati adzabwereko, ndi kudzanditumikira ine mu dziko ili.*

*Ndipo iye anamupatsa iye pangano la mdulidwe: ndipo chotero Abrahamu anabala Isaki, ndipo anamudula iye tsiku lachisanu ndi chitatu; ndipo Isaki anabala Yakobo; ndi Yakobo anabala mbadwa khumi ndi ziwiri.*

<sup>22</sup> Pa malo awa, ife tikukhumba kuti tiyandikire phunziro, limene ine ndikuganiza liri phunziro lopambana la lero, la . . . *Kodi Mzimu Woyera Ndi Chiyani?* Kodi Iwo ndi chiyani? Ndipo, tsopano, chifukwa chimene ine ndatengera phunziro ili mu mzere monga chonchi, iwe sungakhoze kubwera ndi kulandira Mzimu Woyera kupatula iwe utadziwa chimene Iwo uli. Ndipo iwe sungakhoze kuwulandira Iwo, ngati iwe ukudziwa chimene Iwo uli, kupatula iwe ukhulupirire Iwo waperekedwa kwa iwe, ndipo Iwo ndi wa iwe. Ndipo, ndiye, iwe sungakhoze kudziwa ngati iwe uli nawo Iwo, kapena ayi, kupatula iwe ukadziwa zotsatira zomwe Iwo umabweretsa. Kotero ngati iwe udziwa chimene Iwo uli, ndi kuti Iwo ndi wa kwa ndani, ndi machitidwe omwe Iwo umabweretsa pamene Iwo ubwera, ndiye iwe udzadziwa chimene iwe uli nacho pamene iwe uwulandira Iwo. Mwaona? Icho chingakhazikitse basi zimenezo.

<sup>23</sup> Basi monga ine ndinali kuyankhula kwa M'bale wathu Jeffries lero, ndipo iye anati, "Ine ndikanafuna kuti ndidzakhale pa msonkhano usikuuno, koma ine ndidzakhala ndiri kumeneko mawa usiku." Iye sanali kudziwa kuti msonkhano unali ukuchitika, chifukwa ife sitinawulengeze iwo; komwe kuno kokha. Ena a... M'bale Leo ndi iwo analembera kwa ena a abwenzi athu ndipo anawauza iwo, kunjwa kwa mzinda. Chabwino, chifukwa ife tinalibe malo.

<sup>24</sup> Tsopano ine ndinati, "M'bale Jeffries, ngati inu mutandituma ine kumusi kuti ndikayambitse kuyenda chimodzi cha zitsime zanu, ndipo ine nkukhala ndisakudziwa kanthu za izo, ine mwinamwake ndikanachiphulitsa icho. Ine ndikhoza kukapotokola fungulo lolakwika kapena kuyambitsa injini yolakwika. Ine ndikanayenera kudziwa momwe ndingachitire izo ine ndisanachite izo."

Ndipo ndi momwe ziriri ndi kulandira Mzimu Woyera. Iwe uyenera kudziwa chimene iwe ukudzera, ndi momwe iwe ungati uwulandirire Iwo, ndi chimene Iwo uli.

Tsopano, malo oyamba, Mzimu Woyera wakhala utalonjzedwa.

<sup>25</sup> Ife tikanakhoza kutenga masabata khumi ndipo osakhoza... nkungolumpha mu mphepete mwa phunziro ili, chimene Mzimu Woyera uli. Koma, chinthu choyamba, ine ndikufuna kuti ndiliyandikire ilo mokwanira basi kuti tipereke ndondomeko usiku uliwonse, ndiye nkuwona usiku wotsatira ngati pali mafunso aliwonse.

<sup>26</sup> Ndi angati muno amene sanalandire Mzimu Woyera, kukhala atabatizidwa ndi Mzimu Woyera? Kwezani manja anu; inu mukudziwa inu simunakhale muli nawo. Tangoyang'anani pa manjawo.

Tsopano ine ndikufuna kuti ndiyankhule pa Iwo, ngati Mzimu Woyera kukhala chizindikiro, pakuti Iwo uli chizindikiro. Ife tikuzindikira izo, kuti malonjezo onse ali operekedwa kwa ife ndi... Abrahamu anali atate wa lonjezo, chifukwa Mulungu anapereka lonjezo kwa Abrahamu ndi kwa Mbewu yake yapambuyo pa iye. Lonjezo ndi lopangidwa "kwa Abrahamu ndi ku Mbewu yake." Ndipo chizindikiro ichi ndi cha kwa anthu a pangano.

<sup>27</sup> Tsopano, pali kusiyana kwakukulu pakati pa Mkhristu chabe ndi Mkhristu wodzazidwa-Mzimu-Woyera. Ndipo tsopano ife tati tizipeze izi kuchokera mu Lemba, ndi kuzikhazikitsa izo chimodzimidzi basi mu Lemba. Malo oyamba, alipo Mkhristu odzitcha kuti ali Mkhristu. Koma ngati Mkhristu uyu sali atadzazidwa apabe ndi Mzimu Woyera, iye ali chabe mu dongosolo lakuti akhale Mkhristu. Mwaona? Iye akudzinenera kuti akuukhulupirira Iwo; iye akugwirira ntchito kumka ku Iwo, koma Mulungu sanamupatse iye apabe Mzimu uwu, wa Mzimu



Woyera. Iye sanafike apabe malo amenewo ndi Mulungu, kuti Mulungu akuzindikira izo.

<sup>28</sup> Chifukwa, kuti, Mulungu anapanga pangano ndi Abrahamu, atamuyitana kale Abrahamu, chomwe chiri choyimira cha kumuyitana wokhulupirira lero.

Iye anamuyitana Abrahamu, ndipo Abrahamu anasuntha kuchokera mu dziko la kwawo ndipo anapita mu dziko lachirendo, kuti akakhale pakati pa anthu achirendo, ndipo chimenecho chinali choyimira cha pamene Mulungu amuyitana munthu kuti asiye nkhanza zake, kulapa za tchimo lake. Iye amatembenuka ndiye kuchokera ku gulu limene iye analimo, kuti akakhale mu gulu latsopano, pakati pa mitundu yatsopano ya anthu.

Ndiyeno pambuyo pake Mulungu atamupeza Abrahamu kuti anali wokhulupirika ku lonjezo limene Mulungu anamupatsa iye, kuti iye akanadzakhala ndi mwana ndipo kupyolera mwa mwana ameneyu dziko lapansi lonse likanadzakhala lodalitsidwa, ndiye Mulungu anatsimikizira chikhulupiriro chake pa kumupatsa iye chizindikiro, ndipo chizindikiro chimenecho chinali mdulidwe. Ndipo Mdulidwe ndiwo choyimira cha Mzimu Woyera.

<sup>29</sup> Ndime zotsatira chabe za mutu uwu umene ife tangowerenga kumene, ngati inu mukufuna kuti muzilembe izo. Ndipo... Stefano anati, mu ndime ya 51:

*Inu amakosi owuma...osadulidwa mu mtima ndi makutu, inu nthawizonse mumawukaniza Mzimu Woyera: monga makolo anu anachitira, inunso mukutero.*

<sup>30</sup> Mdulidwe uli choyimira cha Mzimu Woyera. Ndipo Mulungu anamupatsa Abrahamu—chizindikiro cha mdulidwe iye atamulandira kale Mulungu pa lonjezo Lake ndi kuyenda kupita mu dziko lachirendo. Mwaona? Icho chinali chizindikiro.

Ndipo ana ake onse, ndi mbewu yake pambuyo pake, imayenera kukhala nacho chizindikiro ichi mu mnofu wawo, chifukwa icho chinali chowasiyanitsa. Icho chinali choti chiwalekanitse iwo kuchokera kwa anthu ena onse, chizindikiro ichi cha mdulidwe.

<sup>31</sup> Ndipo ndicho chimene Mulungu akugwiritsa ntchito lero. Ndi chizindikiro cha mdulidwe wa mtima, Mzimu Woyera, umene ukupangitsa Mpingo wa Mulungu Mpingo wolekanitsidwa kuchokera ku zikhulupiriro zina zonse, zikhulupiriro ndi zipembedzo. Iwo ali mu mitundu yonse ya zipembedzo, komabe iwo ndi anthu opatulidwa. Inu mundilole ine ndiyankhule kwa munthu maminiti awiri, ine ndikhoza kukuuzani inu ngati iye waulandira Mzimu Woyera kapena ayi; chomwechonso inu mukhoza. Iwo umawapatula iwo.

Ndi chilemba. Ndi chizindikiro. Ndipo Mzimu Woyera ndiwo chizindikiro. Ndipo ndiwo . . .

Mwana aliyense yemwe anakakana mdulidwe mu Chipangano Chakale, umene unali mthunzi wotsogolera wa Mzimu Woyera, anali kudulidwa kuchokera pakati pa anthu. Iye samakhoza kukhala nacho chiyanjano ndi osonkhana onse, ngati iye akana kuti adulidwe.

Tsopano fanizitsani zimenezo ndi lero. Munthu yemwe akanati akane kuti alandire ubatizo wa Mzimu Woyera, sangakhoze kukhala nacho chiyanjano pakati pa iwo amene ali nawo Mzimu Woyera. Iwe sungakhoze basi kuchita zimenezo. Iwe uyenera kukhala chikhaliidwecho. Monga, ziri . . .

<sup>32</sup> Mayi anga uko anakakonda kunena kuti, “Mbalame za nthenga zimawuluka limodzi.” Chabwino, ndi mwambi wakale, koma ndiwo umodzi wona. Inu simumaziwona nkhunda ndi akhwangwala zikuyanana. Zakudya zawo ndi zosiyana. Zizolowezi zawo ndi zosiyana. Zokhumba zawo ndi zosiyana.

Ndipo ndi momwe izo ziliri ndi dziko ndi Mkristu pamene iwe wakhala *utadulidwa* ndi Mzimu Woyera, chomwe chimatanthauza, “kudula mnofu kuuchotsapo.”

<sup>33</sup> Mdulidwe umakhoza kukhala mwa mwamuna yekha. Koma ngati mkazi anali atakwatiwa kwa mwamuna, iye amakhala gawo la iye, iye anadulidwa naye iye. Inu mukukumbukira, mu Timoteo, pamene Iwo amanena mmenemo, “Pakutero iye adzapulumutsidwa mu kubala ana, ngati apitirira mu chikhulupiriro ndi chihero ndi ubwino wonse.”

<sup>34</sup> Tsopano, mdulidwe. Inu mukudziwa pamene . . . Sara anaseka mu hema kuseri kwake, pa uthenga wa Mngelo, pamene Iye anati, “Abrahamu,” pokhala osadziwa yemwe iye anali, mlendo, “ali kuti mkazi wako, Sara?” Iye anadziwa bwanji kuti iye anali ndi mkazi?

<sup>35</sup> Monga Yesu anati, “Monga izo zinali mu masiku a Loti, chotero izo zikanati zidzakhale mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Kumbukirani, zizindikiro zimenezo sizinaperekedwe uko ku Sodomu ndi Gomora, mu dziko pakati pa azachipembedzo. Koma izo zinali kwa Osankhidwa, otulutsidwa. Ndipo Abrahamu anayitanidwa kuti atuluke. Ndipo mawu akuti *mpingo* amatanthauza “oyitanidwa kuti atuluke; olekanitsidwa,” monga Abrahamu anadzipatula iyeyekha ndipo anali atadulidwa.

Ndiyeno pamene Sara anaseka pa uthenga umene wa Mngelo, Mulungu akanakhoza kumupha iye pa malopo; koma Iye sakanakhoza kumuvutitsa Sara popanda kumuvutitsa Abrahamu, chifukwa iwo anali amodzi. Iye anali gawo la iye. “Sindinunso awiri, koma mmodzi.”

<sup>36</sup> Kotero, mdulidwe, Mzimu Woyera lero umadula mtima. Ndipo ndi chizindikiro, chizindikiro choperekedwa.

Winawake ananena tsiku lina...Ine ndikungobwereza izi, osati ngati nthabwala. Chifukwa, ndi zoon, koma izo zikumveka ngati nthabwala. Monga ine kawirikawiri ndanena, ano si malo ochitira nthabwala. Koma kunali wachi Germani wamng'ono kunjira ku Gombe Lakumadzulo, kumene ife tinaliko posachedwa. Iye analandira Mzimu Woyera. Ndipo iye anapita chotsika mu msewu, ndipo iye amakhoza kuyenda kamtunda kakang'ono, ndipo iye amakhoza kukweza mmwamba manja ake ndi kuyankhula mu malirime. Ndipo iye amakhoza kuthamanga, ndipo iye amakhoza kulumpha, ndipo iye amakhoza kufuula. Ndipo iye anali ku ntchito, akumapitirizabe monga choncho, ndipo bwana wake ananena kwa iye, “Kodi iwe wakhala uli kuti?” Ine—ine ndimawakonda malo amenewo kumene iwe wakhala uli. Iye anati, “Iwe uyenera kuti unali uko pakati pa gulu la manati lija.”

Iye anati, “Ndiye inu mukuganiza kuti iwo ndi manati?”

Iye anati, “Zedi, iwo ali.”

<sup>37</sup> Iye anati, “Chabwino, Ambuye alemekezeke chifukwa cha manati!” Ndipo iye anati, “Inu mukudziwa chiyani? Manati amachita gawo lalikulu.” Iye anati, “Mwa chitsanzo, galimoto, inu mukachotsamo manati onse mwa iyo, inu simutsala ndi kanthunso koma mulu wa ‘chiphakasa.’” Kotero ndiko pafupi kulondola basi.

<sup>38</sup> Iwe ndiwe wosiyana kwambiri pamene Mzimu Woyera ubwera pa iwe, mpaka malingaliro a dziko lino samakukonda iwe, ndipo iwo amatsutsana nawe iwe, ndipo iwo samafuna kalikonse koti azichita ndi iwe, nkomwe. Ndiwe wobadwira mu Dziko lina. Iwe ndiwe mochuluka basi monga mlendo, nthawi khumi mlendo mochuluka momwe iwe ukanakhalira, ngati iwe ukanapita mu zigawo zikutali za nkhalango za Afrika. Iwe umakhala wosiyana pamene Mzimu Woyera ubwera, ndipo Ndiwo chizindikiro. Ndiwo chilemba pakati pa anthu.

<sup>39</sup> Tsopano, inu mukuti, “Ndiye, M'bale Branham, chizindikiro chija cha mdulidwe chinaperekedwa kwa Abrahamu?” Izo nzoona. “Ndi kwa Mbewu yake?” Inde.

<sup>40</sup> Chabwino, tsopano ife tati titsegule ku Agalatia, mutu wa 3, ndime ya 29, ndipo tiwone momwe izo zikanakhoza kutengedwera kwa ife. Agalatia 3:29, ndipo tingowona momwe mdulidwe uwo ukanakhoza kutengedwera kwa Amitundu, ngati ife tiri Amitundu; chimene, mwa kubadwa kwachilengedwe ife tiri.

Tsopano, poyamba, ine ndikufuna kuti ndiwerenge ndime ya 16.

*Tsopano kwa Abrahamu ndi mbewu yake lonjezo linapangidwa. (Abrahamu ndi mbewu yake!) Iye sanati ayi, Ndi kwa mbewu zake, . . .*

Kungoti mtundu uliwonse wa . . . mukuti, “O, ine ndine mbewu za Abrahamu, inenso.” Ayi. Kwa “Mbewu,” Mbewu ya Abrahamu!

*. . . Osati kwa mbewu, ngati za ambiri; koma ngati ya mmodzi, Ndipo kwa—kwa iwo . . . Ndipo kwa mbewu yako, yomwe ili Khristu.*

<sup>41</sup> Khristu anali Mbewu ya Abrahamu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, tsopano tiyeni titenge ndime ya 28 ndi 29.

*Palibe Myuda kapena Mhelene, ngakhalenso palibe wansinga kapena mfulu, ngakhalenso palibe mwamuna kapena wamkazi: pakuti ife ndife tonse amodzi mwa Khristu Yesu.*

*Ndipo ngati inu muli a Khristu, ndiye inu ndinu mbewu ya Abrahamu, ndipo ndinu olova molingana ndi lonjezo.*

Ife timayitenga bwanji “Mbewu ya Abrahamu”? Pa kukhala mwa Khristu, ndiye ife ndife Mbewu ya Abrahamu. Ndipo kodi Mbewu ya Abrahamu inali chiyani? Monga, ife tikanati tipitirire mpaka ku Aroma 4 ndi malo osiyana.

Abrahamu sanalandire konse lonjezo pamene iye anali wodulidwa. Kusonyeza kuti mdulidwe unali choyimira chabe, iye analandira lonjezo *mmbuyo* iye asanadulidwe. Ndipo ilo linali choyimira, cha kuzindikiridwa kwa chikhulupiriro chake chimene iye anali nacho iye asanadulidwe.

<sup>42</sup> Tsopano, pamene ife tiri mwa Khristu, ife timakhala Mbewu ya Abrahamu ndipo ndife olova naye Khristu, chotero, ziribe kanthu yemwe ife tiri, Myuda kapena Wamitundu.

Ndipo, “Mbewu ya Abrahamu,” Mbewu ya Abrahamu ili nacho chikhulupiriro cha Abrahamu, omwe amamutenga Mulungu pa Mawu Ake. Mosasamala momwe Iwo akuwoneka mopusa, mosazolowereka momwe iwe uchitira mwachirendo, momwe Iwo amakupangitsira iwe, iwe umamutenga Mulungu pa Mawu Ake mosasamala za chirichonse.

<sup>43</sup> Abrahamu pa usinkhu wa makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu, ndi Sara wa makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu, anamutenga Mulungu mwa Mawu Ake, ndipo anatcha chirichonse chosiyana kwa Iwo ngati kuti panalibepo. Kodi inu mukuganiza madokotala ankaganiza chiyani, a tsiku limenelo? Kodi inu mukuganiza anthu ankaganiza chiyani, pamene iwo anamuwona munthu wachikulire, zaka makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu zakubadwa, akupita paliponse akuyamika Mulungu, iye amati “akhala ndi mwana” ndi

mkazi wake, ndipo iyeyo wa zaka makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu zakubadwa, pafupi zaka makumi awiri ndi zisanu atadutsa posiya zaukazi? Koma, inu mukuona, izo zimakupangitsa iwe kuchita moseketsa, chikhulupiriro cha Abrahamu.

<sup>44</sup> Ndipo pamene iwe uli wodulidwa ndi Mzimu Woyera, Iwo umachita chinthu chomwecho kwa iwe. Iwo umakupangitsa iwe kuchita zinthu zomwe iwe sumaganiza kuti iwe ukanazichita. Iwo umakupangitsa iwe kutenga lonjezo la Mulungu ndi kumukhulupirira Mulungu.

<sup>45</sup> Tsopano, Iwo ulinso, pambali pa—lonjezo ndi chizindikiro, Iwo ulinso chisindikizo. Tsopano ngati inu muti mupite ndi ine mpaka ku Aroma. Choyamba, ine ndikufuna inu mupite ndi ine ku Aefeso 4:30, ndipo tiyeni tiwerenge apa miniti chabe. Aefeso 4:30 akunena izi.

Tsopano, inu mwawamvapo anthu ambiri akunena kuti zinthu zosiyana ziri zisindikizo. “Ngati inu mulowa mu mpingo, inu mumakhala ndi chisindikizo cha mpingo.” Ndipo anthu ena amati, “Icho ndi kusunga tsiku lina lake, tsiku la sabata, ndicho—ndicho chisindikizo cha Mulungu.” Ena a iwo amati, “Ngati ife tiyika umembala wathu mu chipembedzo chinachake, ife timasindikizidwa kulowa mu Ufumu wa Mulungu.”

<sup>46</sup> Tsopano, Baibulo linati, “Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, ndipo a Mulungu akhale Choonadi.” Tsopano, Aefeso 4:30 akuwerengeka monga chonchi:

*Ndipo musakwiyitse ayi Mzimu woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo kufikira tsiku la chiwombolo.*

<sup>47</sup> Ine ndichita kutenga molimba pang’ono pa izi tsopano, kuyala pansi. Tsopano, inu abale mwamalamulo ingkhalani chete kwa pang’ono pokha. Mwaona? Kodi inu munazindikira utali womwe chisindikizo chimenecho chimathera? Osati mpaka ku chitsitsimutso chotsatira, mpaka nthawi yotsatira pamene chinachake chichitike molakwika. “Mpaka tsiku la chiwombolo chako,” ndiwo utali womwe iwe umasindikizidwira. “Mpaka tsiku la chiwombolo chako,” pamene iwe uli woomboledwa kuti ukakhale ndi Mulungu, ndiwo utali womwe Mzimu Woyera umakusindikizira iwe. Osati kuchokera ku chitsitsimutso kukafika ku chitsitsimutso; koma kuchokera ku Muyaya mpaka ku Muyaya, iwe uli wosindikizidwa ndi Mzimu Woyera.

Ndicho chimene Mzimu Woyera uli, Iwo ndi chisindikizo cha Mulungu, kuti Iye wapeza . . . iwe wapeza chisomo pamaso Pake, ndipo Iye akukukonda iwe, ndipo Iye akukukhulupirira iwe, ndipo Iye wayika chisindikizo Chake pa iwe. Kodi chisindikizo ndi chiyani, aliyense? Bwanji, *chisindikizo* chimakhazikitsa kapena chimatanthawuza “ntchito yotsirizidwa.” Ameni. Mulungu wakupulumutsa iwe, wakuyeretse iwe, wakutsuka

iwe, wapeza chifundo ndi iwe, ndipo wakusindikiza iwe. Iye watsirizitsa. Ndiwe chotuluka mwa Iye Chake mpaka tsiku la chiwombolo chako. *Chosindikizidwa* ndi “chinthu chotsirizidwa.”

Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Iwo ndi chizindikiro. Ife tifika pa zimenezo kanthawi kena, mu Uthenga wina, chizindikiro chimene Paulo anachikamba. Malirime anali chizindikiro kwa okhulupirira . . . kapena osakhulupirira.

<sup>48</sup> Tsopano zindikirani, koma, mu ichi, Mzimu Woyera ndi chizindikiro. Ine ndikutanthauza. . . Ndipo Mzimu Woyera ndiwo chisindikizo. Iwo ndi chizindikiro chimene Mulungu anapereka kwa ana Ake osankhidwa. Kuwukana Iwo, ndi kuti udulidwe kuchoka kwa anthuwo; ndipo kuwulandira Iwo, ndi kukhala utatsirizana nalo dziko ndi zinthu zonse za mdziko, ndi kukhala chinthu chomwe Mulungu wayikapo chisindikizo cha kuvomereza.

<sup>49</sup> Ine kale ndinkagwira ntchito ku njanji kunja kuno ku Harry Waterberry, ndipo ife tinkakhoza kupita kumusi kuti tikalongeze magalimoto. M'bale wanga, Doc, wayima kumbuyo ukoyo, amathandizira kulongeza magalimoto. Pamene galimoto ikulongezedwa, iwo amapita modutsa galimoto imeneyo, wofufuza, ndipo ngati iye apeza chirichonse chogwedera, pamene iyo ingakhoze kugwa ndi kusweka, kapena chirichonse chimene chikanakhoza kuwononga; iye sakanati ayisindikize galimoto imeneyo mpaka galimoto imeneyo ili yolongezedwa kwathunthu, mpaka iyo ili yolongezedwa chotero pansu ndi mwa dongosolo chotero, kuti kugwedera kwa kukwera sikuti kuvutitse zinthu zimene ziri mkatimo.

<sup>50</sup> Ndilo lomwe liri vuto kuti ife sitimakhala osindikizidwa kwambiri chotero; ndife ogwedera kwambiri nazo zinthu. Pamene Wofufuza akupita chodutsa, kuti afufuze moyo wanu, kuti awone ngati inu simuli ogwedera pang'ono chabe nazo zinthu, wogwedera pang'ono nawo moyo wanu wa pemphero, wogwedera pang'ono nako kupsya mtima kuja, wogwedera pang'ono nalo lirime limenelo, poyankhula za ena, Iye sadzaisindikiza konse galimoto imeneyo. Zizolowezi zina zoyipa, zinthu zina zauthakati, malingaliro ena auve, Iye sangakhoze kuisindikiza galimotoyo.

Koma pamene Iye achipeza chirichonse mu malo ake, Wofufuza, ndiye Iye amayisindikiza iyo. Asayese wina kuyerekeza kuchitsegula chisindikizo chimenecho mpaka galimoto imeneyo itafika kumene iyo ikupita kumene iyo yasindikiziridwira! Ndi imeneyo apo. “Musati mukhudze wodzozedwa Wanga; musawachitire aneneri Anga chowapweteka ayi. Pakuti ine ndikuti kwa inu, izo zikanakhala bwino kwa inu kuti mphero ikanati imangidwe pa khosi panu, ndipo inu mukanati muponyedwe mwa kuya kwa nyanja, kuposa

ngakhale kuti inu muyesere kukwiyitsa kapena kugwedeza pang’ono pa aang’ono a awa omwe akhala atasindikizidwa.” Kodi inu mukuona chimene icho chikutanthauza?

<sup>51</sup> Ndicho chimene Mzimu Woyera uli. Ndiwo chitsimikiziro chanu. Ndiwo chitetezero chanu. Ndiwo umboni wanu. Ndiwo chisindikizo chanu. Ndiwo chizindikiro chanu, kuti, “Ndine womka Kumwamba. Mopanda kusamala zimene mdierekezi akunena! Ndine womka Kumwamba. Chifukwa chiyani? Iye anandisindikiza ine. Iye anawupereka Iwo kwa ine. Iye anandisindikizira ine kulowa mu Ufumu Wake, ndipo ndine Womka-kuulemerero! Lekani mphepo iwombe, lekani Satana achite zimene iye akufuna kuchita. Mulungu wandisindikiza kale ine mpaka tsiku la chiwombolo changa.” Ameni! Ndicho chimene Mzimu Woyera uli. O, inu muyenera kumawufuna Iwo. Ine sindikanakhoza kumapitirirabe wopanda Iwo. Zochuluka kwambiri zikanakhoza kunenedwa pamenepo, koma ine ndikutsimikiza inu mukudziwa chimene ine ndikuchikamba.

<sup>52</sup> Tsopano, ndiponso, tiyeni ife titembenuzire ku Yohane 14, kwa miniti chabe. Ine ndimangowakonda Mawu! Ndiwo Choonadi.

<sup>53</sup> Tsopano, Mzimu wa Mulungu, Mzimu Woyera, kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Iwo ndiwo Mzimu wa Khristu mwa inu. Tsopano, ife tisanati tiwerenge, ine ndikanafuna kuti ndinene mawu pang’ono ochitira ndemanga apa. Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Iwo ndi chisindikizo. Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Iwo ndi pangano. Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Iwo ndi chizindikiro. Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani ndiye? Ndiwo . . . Mzimu wa Yesu Khristu mwa iwe. Mwaona? “Kanthawi pang’ono,” anatero Yesu, “ndipo dziko silindiwonanso Ine; komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndiri ndi inu, ngakhale mkati mwa inu, mpaka ku mapeto a dziko.” Mzimu wa Mulungu mu Mpingo Wake!

<sup>54</sup> Wa chiyani? Kodi Iye anachitiranji izo? Izi ndi pang’ono za phunziro la mawa usiku. Koma kodi Iye anachitiranji izo? Nchifukwa chiyani Iye anachita, nchifukwa chiyani Mzimu Woyera . . . Chiyani, kodi Iye anadzera chiyani? Kodi Iye anabwereranji mkati mwa inu, kodi Iye anabwereranji mkati mwa ine? Zinali kuti adzapitirize ntchito za Mulungu.

<sup>55</sup> “Ine nthawizonse ndimachita izo zimene ziri zokondweretsa kwa Atate Anga. Ine sindinabwere kuti ndidzachite chifuniro Changa changa, koma cha Atate omwe anandituma Ine. Ndipo Atate amene anandituma Ine ali ndi Ine; ndipo monga Atate Anga andituma Ine, chotero Ine ndikukutumani inu.” O, mai! [M’bale Branham akuwombetsa manja ake pamodzi kawiri—Mkonzi.] Atate anamutuma Iye, anapita mkati mwa Iye. Atate omwe anamutuma Yesu anabwera mkati mwa Iye, ankagwirira ntchito kupyolera mwa Iye.

Yesu amene amakutumani inu, amapita ndi inu ndipo ali mkati mwa inu. Ndipo ngati Mzimu umenewo, wokhala moyo mwa Yesu Khristu, unamupanga Iye kupanga ndi kumachita momwe Iye ankachitira, inu mukhala nalo lingaliro lina wamba momwe Iwo uti uzichitira pamene Iwo uli mkati mwa inu, chifukwa Moyo umenewo sungakhoze kusintha. Iwo uzipita kuchokera mu thupi kupita ku thupi, koma Iwo sungakhoze kusintha chikhalidwe Chake, pakuti Iwo ndiwo Mulungu.

<sup>56</sup> Tsopano mu Yohane 14, basi tiyeni tingowerenga pang'ono pokha, kuyambira pa ndime ya 10.

*Ukhulupirira iwe...kuti Ine ndiri mwa Atate, ndipo Atate mwa ine? ntchito...mawu amene Ine ndiyankhula kwa inu Ine sindikuyankhula mwa inendekha: koma Atate amene akukhala mkati mwa ine, iye akuchita ntchitozo. (Taganizani za zimenezo tsopano.)*

*Khulupirirani ine kuti Ine ndiri mwa Atate, ndi Atate mwa ine: kapena mwina ndikhulupirireni ine chifukwa cha ntchito zomwezo.*

*Indetu, indetu, Ine ndinena kwa inu, Iye amene akhulupirira pa ine, ntchito zimene Ine ndizichita iyenso adzachita...nayenso; ndipo ntchito zazikulu zoposa izo iye adzazichita; chifukwa ine ndikupita kwa Atate anga.*

Kodi inu simukuwona? Mukuona momwe Iye ananenera pamenepo? Tsopano penyani izi, momwe izi zikutulukira. Ine ndiwerenga mopitiriza pang'ono chabe. Ife tati tiwerenge mmusi pafupi mpaka ndime ya 20. “Ndipo chirichonse chimene inu muti mudzapemphe mu...” Tiyeni tiwone, ine ndinali... Eya. U-nhu. Chabwino.

*Ndipo chirichonse inu muti mudzapemphe mu dzina langa, chimenecho ine ndidzazichita, kuti Atate akhoze kumalemekezedwa mwa Mwana.*

*Ngati inu muti mudzapemphe chirichonse mu dzina langa, Ine ndidzazichita icho.*

*Ngati inu mundikonda ine, sungani malamulo anga.*

*Ndipo Ine ndidzawapempha Atate, (tsopano penyani) ndipo iwo adzakupatsani inu Mthonhozi wina, kuti iye akhoze kukhala ndi inu kwa nthawizonse;*

*Ngakhale Mzimu wa choonadi; amene dziko silingakhoze kumulandira, chifukwa ilo siliri kumuwona iye ayi, ngakhale kumudziwa iye: koma inu mukumudziwa iye; pakuti iye wakhala ndi inu, ndipo adzakhala ali mkati mwa inu.*

<sup>57</sup> Mzimu ameneyo ndi ndani ndiye? Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Ndi Khristu mkati mwa inu. Mthonhozi, ndiye



Mzimu Woyera. “Ndipo pamene Mtonthozi adza, Iye adzachita zinthu zomwezo zimene Ine ndazichita pamene Mtonthoziyo ali mwa Ine. Ine ndiwapempha Atate, ndipo Iye adzakupatsani inu Mtonthozi uyu. Inu mukumudziwa Mtonthoziyo. Dziko silikumudziwa Iye, ngakhale silidzamudziwanso. Koma inu mukumudziwa Iye chifukwa Iye wakhala tsopano ndi inu,” Yesu akuyankhula, “koma Iye adzakhala mkati mwa inu.” Ndi inu pamene, ndiye Mtonthoziyo, “adzakhala ali mkati mwa inu.”

*Ine sindidzakusiyani inu osatonthozedwa: Ine ndidzadza kwa inu.*

“Ine sindidzati ayi. . .” Tsopano, uyo ndiwo Mtonthozi, Khristu. Ndicho chimene Mzimu Woyera uli, ndi Khristu.

*Komabe kanthawi pang’ono, ndipo dziko silindiwonanso ine; koma inu mudzandiwona ine: chifukwa ine ndiri moyo, inu. . . mukhala moyo nanunso.*

<sup>58</sup> O, ife tikhoza kumangopitirira pitirira; koma, kuti ndikudziwitseni inu. Kodi Iye ndi chiyani? Iye ali chisindikizo. Iye ali chizindikiro. Iye ali Mtonthozi. Mukuona zonse zomwe Iye ali? Mbewu ya Abrahamu inalandira Iwo.

<sup>59</sup> Tsopano tiyeni panonso tipeze kuti. . . nchiani chinanso Mtonthozi ali. Tiyeni tipite ku Yohane Woyamba 16:7, tikawone ngati Iye sali Woyimira mulandu, ndiponso. Inu mukudziwa chomwe woyimira mulandu ali, kuyimira mulandu. Ife tiri naye Wotiyimira mulandu. Ife tikudziwa zimenezo. Yohane Woyamba mutu wa 16. . . O, dikirani miniti, ine ndikupepesa. Yohane Woyera, iye ali, 16:7. Ine ndikupepesa. Ine ndithu ndikupepesa kuti ine ndinanena izo. Ine ndinawerenga izo molakwitsa pa langa. . . ndapapeza 16:7.

*Komabe Ine ndikuzani inu choonadi; Kuli koyenera kwa inu kuti Ine ndichokepo: chifukwa ngati ine sindichokapo, Mtonthozi sadzabwera kwa inu; koma ngati Ine ndichoka, Ine ndidzamtumiza iye kwa inu.*

*Ndipo pamene iye abwera, iye adzalitsutsa dziko za tchimo, ndi za chilungamo, ndi za chiweruzo:*

*Za tchimo, chifukwa iwo sanakhulupirire pa ine;*

*Za chilungamo, chifukwa Ine ndikupita kwa Atate, ndipo inu simudzandiwonanso ine;*

*Za chiweruzo, chifukwa kalonga wa dziko lino ndi woweruzidwa.*

<sup>60</sup> Mai! Tsopano, Woyimira mulandu, akupezeka mu—mu Yohane Woyamba 2:12. Tsopano tiyeni tiwerenge zimenezo, miniti chabe, Yohane Woyamba 2:12. Ine ndikupempha kukhululukira kwanu, Yohane Woyamba. . . 1 ndi 2, izo ziri. Ine ndiri nazo izo zitalembedwa, Yohane Woyamba 2:1 mpaka 2.

*Ana Anga aang'ono, zinthu izi Ine ndikulemba kwa inu, kuti inu musachimwe ayi. Ndipo ngati munthu aliyense achimwa, ife tiri naye wotiyimira mulandu nawo Atate, Yesu Khristu wolungamayo:*

Woyimira mulandu ndi ndani? Yesu Khristu wolungamayo.

*Ndipo iye ali—iye ali chitetezero cha machimo athu: ndipo osati wa athu okha, komanso wa machimo a dziko lonse.*

<sup>61</sup> Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Iwo ndi Woyimira mulandu. Umachita chiyani. . . Woyimira mulandu ndi chiyani? Kodi Iwo umachita chiyani? Umapanga kuyimira mulandu. Iwo uli nacho chifundo. Iwo, Iwo umayima mu malo anu. Iwo, Iwo umachita zinthu zimene inu sumungakhoze kuzichita. Iwo, Ndiwo—Iwo ndi chitetezero cha machimo anu. Ndiwo chilungamo chanu. Ndiwo machiritso anu. Ndiwo Moyo wanu. Ndiwo chiwukitsiro chanu. Ndiwo zonse zimene Mulungu ali nazo kwa inu. Iye ndi Woyimira mulandu.

<sup>62</sup> Momwe ife tikanakhoza kupitira mwa dongosolo ndi izo ndi kuziswera izo pansu, za momwe pamene Iwo—Iwo umapangira chitetezero chifukwa cha kusadziwa kwathu. Nthawizina pamene. . . ife tiri nawo Mzimu Woyera, ife mwaumbuli timadzandimira mu chinachake. Mzimu Woyera uli pamenepo kuti uyimire mulandu kwa ife. Iye ali Wotiyimira mulandu wathu. Iye amayima wathu. . . Iye ndi Wotiyimira wathu. Iye amayima pamenepo ndi kumatichonderera ife. Iye sitimadzichonderera tokha, chifukwa Mzimu Woyera mwa ife umatichonderera ife. Mzimu Woyera umapereka maneno, nthawizina ndi mawu amene iwe sungakhoze kuwamvetsa, ndipo Iye amapangira chitetezero kwa ife. Ndicho chimene Mzimu Woyera uli.

<sup>63</sup> Pamene ine ndiyenda kulowa mu chirichonse, ine—ine ndimayenda ngati mwana wamng'ono; inu mumayenda ngati mwana wamng'ono. Ife, ife tikuyenda mu dziko la mdima lodzaza ndi adani, lodzaza ndi tchimo, lodzaza ndi misampha, lodzaza ndi chirichonse.

Inu mukuti, “O, ine ndikuchita mantha. Ine ndikuchita mantha kuti nditenge moyo wa Chikhristu. Ine, ine ndikuchita mantha kuti ndichite *izi*. Ine ndikuwopa ine ndingadzachite *izi*.”

Musati muzichita mantha. Ife tiri naye Wotiyimira mulandu. Ameni. O, Iye amayima pafupi nafe. Iye ali mwa ife, ndipo Iye amachitira chitetezero ife. Mzimu Woyera, mowirikiza, mowirikiza kuyimira mulandu wa ife, nthawi zonse. Iye ndi Wotiyimira mulandu wathu. O, momwe ife tikumuthokozera Mulungu chifukwa cha izo!

<sup>64</sup> Chisindikizo, chizindikiro, Mzimu wa Moyo, Mulungu wa Kumwamba, Mtonthozi, Moyo, Woyimira mulandu. Kodi Iye ndi chiyani! O, mai! Ife tikhoza kupitirira kwa maora ndi izo.

<sup>65</sup> Tsopano ife tati tisinthe kwa miniti yokha. Tsopano ife tati tifunse tsopano. . .

Analonjeza kwa ife mu masiku otsiriza! Woyimira mulandu uyu, chisindikizo, lonjezo, chirichonse chimene ife takamba zokhudza Iye usikuuno, ndi zikwi khumi kuchulukitsa zoonjezerapo, Iwo unapangidwa lonjezo kwa ife mu tsiku lotsiriza.

Iwo analibe Iwo mu tsiku limenelo. Iwo anangokhala ndi chisindikizo mu mnofu wawo, monga chizindikiro ndi chisonyezo, kukhulupirira kuti Iwo unali kudza, ndipo iwo ankayenda mwa mthunzi wa lamulo. Chimene, iwo ankadulidwa mu mnofu.

<sup>66</sup> Lero ife sikuti timayenda mwa mthunzi wa lamulo. Ife timayenda mwa mphamvu ya chiwukitsiro. Ife tikuyenda mwa mphamvu ya Mzimu, Umene uli chisindikizo chathu choona, Wotiyimira mulandu wathu wooka, Mtonthozi wathu wooka, chizindikiro chathu choona kuti ife tabadwa kuchokera Kumwamba; achilendo, anthu osamvetseka, ochita moseketsa, omutenga Mulungu pa Mawu Ake, kuchitcha china chirichonse cholakwika. Mawu a Mulungu ndi owona. Ndizo. . . O, mai! Ndicho chimene Mzimu Woyera uli.

<sup>67</sup> Kodi inu mukuwufuna Iwo? Kodi inu simukanakonda kuti mukhale nawo Iwo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Tiyeni tiwone ngati Iwo uli wolonjezedwa.

Tsopano tiyeni tibwerere ku Yesaya, Bukhu la Yesaya. Tiyeni titenge mutu wa 28 wa Yesaya. Tsopano ife tikupita ku Yesaya 28, ndipo ife tikayambira pafupi. . . Tiyeni titenge ndime ya 8, tiwone chimene Yesaya ananena, zaka mazana asanu ndi awiri mphambu khumi ndi ziwiri Iwo usanabwere.

<sup>68</sup> Ife tikhoza kunena zochuluka za izi, kubwerera, njira yonse mmbuyo, koma ife tingoyambira pano pomwe ndi kuwona ngati Iwo unalonjezedwa kwa Mpingo. Kodi ndi tsiku lanji limene Iwo unali kuyenera kuti ubwere? Pa masiku otsiriza, pamene apo pati padzakhale—chivundi. Tsopano kumbukirani, mawuwo ali mochulukitsa, “masiku,” masiku awiri otsiriza, zaka zikwi ziwiri zotsiriza.

Tsopano, tsopano ndime ya 8.

Onse, *pakuti magome onse ali odzaza ndi. . . nyansi, kotero kuti palibe malo oyera.*

<sup>69</sup> Fufuzani konsekonse lero kuti muwapeze iwo. Kayang’aneni pozungulira ndipo muwone ngati ife tiri mu tsiku limenelo. “Magome onse!” Bwanji, iwo amapita ku Mgonero wa Ambuye, ndipo chinthu choyamba, mu mzere wa zinthu, kutenga kachidutswa kakale ka mkate wopyapyala kapena chikondamoyo, ndi kuchinyema icho ndi kupanga mgonero. Pamene, izo ziyenera kuti zizipangidwa ndi manja a Mzimu

Woyera, ndi mkate wopanda chotupitsa. Khristu sali wauve ndi wanyansi, ndipo iwo umamuyimira Iye.

<sup>70</sup> Chinthu china, iwo amawupereka iwo kwa anthu omwe amamwa, kunama, kuba, kusuta, kutafuna, (psyii!) basi chirichonse, malingana ngati iwo ali a mu mpingo. Zikhale kutali izo! Ngati munthu atatenga konse iwo pamene ife tiri kudya iwo pano, iye akudzipumira ndi kudzimwera chiwonongeko kwa iyemwini, pokhala osalizindikira Thupi la Ambuye. Ngati iye sakhala moyo, akhale kutali kwa iwo.

Ndipo ngati iwe suli kutenga iwo, izo zimasonyeza kuti chikumbumtima chako chomwe chiri cholakwa. “Iye yemwe sadya, alibe gawo ndi Ine,” Yesu anatero.

<sup>71</sup> Koma magome onse a Ambuye asanduka odzaza ndi nyansi. Palibe malo amodzi oyera. Mvetserani, ngati izo sizikujambula lero!

*Kodi iye adzati...kodi iye adzamuphunzitsa ndani chidziwitso? ndipo kodi iye adzamupangitsa yani... kumvetsa chiphunzitso?...*

*...Ndani ati adzamvetse chidziwitso?...kodi iye angakhoze kumupangitsa ndani kuti amvetse chiphunzitso?...*

“Chabwino, Mulungu adalitsidwe, ndine Mpresibateria. Ndine Mmethodisti. Ndine Mpetekoste. Ndine Mnazereni. Ndine wa Pilgrim Holines.” Zimenezo sizitanthauza chinthu chimodzi kwa Mulungu; gome lina chabe.

*...ndani ine nditi ndidzamudziwitse chiphunzitso?...*

<sup>72</sup> Chiphunzitso cha mtundu wanji; Methodisti, Baptisti, Chipresibateria, Chipentekoste? Chiphunzitso cha Baibulo!

*...ndani ine nditi ndidzamudziwitse chiphunzitso?...*

<sup>73</sup> Iwe umadziwa motani pamene iwe waulandira Iwo? Ife tidzafika mu zimenezo Lachisanu usiku. Mwaona?

*...ndani ine nditi ndidzamudziwitse chiphunzitso? (tsopano penyani) iwo amene achotsedwa ku mkaka, ndi kuchotsedwa ku maere.*

<sup>74</sup> Ana aang’ono amati, “Chabwino, ine ndimapita ku mpingo, mayi anga anali a mpingo uwu.” Ine ndiribe kanthu kotsutsa zimenezo, m’bale wokondedwa. Ndipo ine ndikuzindikira kuti izi ali kuzijambula. Izo zonse nzabwino, kukhala wa mpingo wa amayi. Koma, mvetserani, amayi ankayenda mu kuwala kumodzi, iwe ukuyenda mu kuwala kwina.

<sup>75</sup> Lutera anayenda mu kuwala kumodzi; Wesile anayenda mu kwina. Wesile anayenda mu kuwala kumodzi; Pentekoste inayenda mu kuwala kwina. Koma ife tikuyenda mopitirira

pamwamba kuposa izo lero. Ndipo ngati ulipo m'badwo wina, iwo udzapita kupitirira ife.

<sup>76</sup> Kubwerera mu masiku oyambirira, pamene chinthucho chinali chotambalala, kutambalalira kutali, Lutera ankaphunzitsa kulungamitsidwa ndi chikhulupiriro. Izo zinali zoti zingowabweretsa anthu kuchokera ku Chikatolika kupita mu Chiprotestanti, kupita mu chiyanjano pozungulira Mawu. Kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro, zimenezo zinali dera lotambalala lalikulu. Iwo sanasunthe konse kuchoka ku chimenecho.

<sup>77</sup> Motsatira kunadza chitsitsimutso china chotchedwa Joni Wesile. Icho chinawagwedezera iwo pansi kuchoka ku icho, ndipo chinamubweretsa iye pansi ku kuyeretsedwa, kusiya... moyo wabwino, waukhondo, woyera, woyeretsedwa mwa Mawu a Mulungu, kupereka chisangalalo mu mtima mwanu. Chimenecho chinagwedeza mochuluka kwambiri za chiphunzitsa cha Chilutera.

<sup>78</sup> Ndiye potsatira panadza Achipentekoste ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo unazichepetsera izo pansi kachiwiri, mwa kulandira Mzimu Woyera. Ndiko kulondola.

Ndipo tsopano zimenezo zayamba kugwedezekera pansi. Ndipo mphatso, ndi kubwezeretsa, ndi Mzimu wa Mulungu zabwera mkati, mwa chidzalo cha zizindikiro ndi zodabwitsa, mu Mpingo, ndipo zagwedeza Pentekoste. Ndi chiyani icho? Ife tiri pafupi kwambiri ku Kudza kwa Ambuye Yesu, mpaka kuti Mzimu womwe umene unali mwa Iye ukugwira ntchito mu Mpingo, ukuchita ntchito zomwezo zimene Iye ankachita pamene Iye anali pano pa dziko lapansi. Izo sizinayambe zakhala kulikonse, mmbuyo kuchokera ku nthawi ya atumwi mpaka nthawi ino.

Chifukwa chiyani? Mwaona, ndi zotambalala; zimachepera, chepera, chepera. Ndi chiyani icho? Kungokhala monga dzanja lanu likubwera ku mthunzi; chithunzi, chithunzi, chithunzi. Koma ndi chiyani icho? Ndi chinyezimiritso. Lutera anali chiyani? Chinyezimiritso cha Khristu. Wesile anali chiyani? Chinyezimiritso cha Khristu.

<sup>79</sup> Penyani, m'badwo wa Billy Sunday wangotha kumene. Tsiku lina, Dr. Whitney wachikulire, anaphunzitsa pomwe pano pa guwa ili, mmodzi wotsiriza wa sukulu yakale, anamwalira, ali makumi asanu ndi anayi, ine ndikuganiza. Billy Sunday anali wachitsitsimutso kwa mipingo mwadzina mu tsiku lake. Iye sankabweza nk'honya ayi; kuyimirira pamenepo ndi kufuula, "Nonse a inu Amethodisti pitani ku kanjira ka utuchi, alaliki ndi onse! Nonse a inu Abaptisti pitani ku kanjira ka utuchi! Inu Achipresbateria!" Iye sankabweza nk'honya ayi. Iye anali Billy Graham wa tsiku lino.

<sup>80</sup> Zindikirani. Ndiyeno, nthawi yomweyo pamene mpingo mwadzina unali kukhala ndi chitsitsimutso chawo, nchiyani chomwe chinachitika? A Uthenga Wonse anali kukhala ndi chitsitsimutso. Pamenepo panabwera abale a Bosworth, Smith Wigglesworth, ndi Dr. Price, Aimee McPherson, onse amenewo.

Penyani, Smith Wigglesworth anafa usiku umodzi. Dokotala Price anafa usiku wotsatira. Mkati mwa maora makumi awiri ndi anayi ine ndinali pa ntchitoyo.

<sup>81</sup> Tsopano mapeto anga akubwera pano. Yang'anani pa... Inu simukumva zambiri za Billy Graham. Inu simukumva zambiri za Oral Roberts. Ine ndikuwona misonkhano yanga ikuchita mthunzi. Chavuta ndi chiyani? Ife tiri pa mapeto, m'badwo wina.

<sup>82</sup> Kodi Billy Sunday anabwera chotani mkati, ndi iwo? Iwo anabwera mkati chitangotha kumene chitsitsimutso chachikulu cha Moody. Kodi Moody anabwera mkati liti? Chitangotha kumene chitsitsimutso cha Knox. Kodi Knox anabwera mkati liti? Chitangotha kumene chitsitsimutso cha Finney. Finney chitatha cha Kalvini, Kalvini chitatha... Chotero, Wesile, ndipo Wesile chitatha cha Lutera. Mpaka mmusi kupyola m'badwo izo zimabwera. Mwamsanga pamene chitsitsimutso chimodzi chatha, Mulungu amawutsa wina ndi kuponyerapo Kuwala kochuluka; basi kumangopitirira kusuntha monga choncho.

<sup>83</sup> Tsopano ife tiri pa mapeto a nthawi ino. Munthu aliyense wayang'anira pa mathero a mphambano yake Kudza kwa Khristu, koma iwo anali nazo zochuluka zoti ayang'anire mtsogolo; kubwerera kwa Ayuda, mbale zowuluka mu milengalenga, zinthu zonse zimene ife tikuziwona lero. Koma ife tiri pamapeto. Ife tiri pano tsopano. Iwo ankadziwa kuti Mpingo unali woti udzalandire Mphamvu yomwe ikanati idzagwire ntchito mu Mpingo ntchito zomwezo za Khristu, chifukwa ndi pamene mthunzi ukukhala mwakuya ndi mwakuya, ndi kunyezimiritsa mochuluka.

<sup>84</sup> Inu mukawutenga mthunzi. Mtunda wawutali kuchokera ku mthunziwo, mumapeza kunyezimirira kochepe kwa mthunziwo. Pakapita kanthawi, mthunziwo umayandikira yandikira, mpaka mtengo ndi mthunzi ziri chinthu chomwecho.

<sup>85</sup> Tsopano, Mzimu wa Mulungu wagwira ntchito pansu pa kulungamitsidwa, pansu pa Lutera; kuyeretsewa, pansu pa Wesile; ubatizo wa Mzimu Woyera, pansu pa Pentekoste; ndipo pano Iwo uli mu tsiku lotsiriza, ukuchita ndi kupanga zinthu zomwezo kumene zomwe Iwo unachita pamene Iwo unali mwa Khristu. Ndi chiyani icho? Mpingo ndi Khristu zakhala Chimodzi.

Ndipo mwamsanga pamene Iwo alumikizana palimodzi, chilumikizo chotsiriza icho, Iwo udzapita kupyola mu mlengalenga, ukufuula. Pamenepo adzabwera Wesile, Lutera,

ndi ena onse a iwo mmbuyo mu masiku amenewo uko, “iye amene ali woyamba adzakhala wotsiriza, iye yemwe ali wotsiriza adzakhala woyamba,” ndiyeno padzabwera chiwukitsiro.

<sup>86</sup> Ife tiri pa mapeto a nthawi. Mvetserani, ndicho chimene Mzimu Woyera umachita. Mzimu Woyera, mwa kulungamitsidwa, onani, mthunzi pang’ono chabe wa Iwo; Mzimu Woyera, mwa kuyeretsedwa, mthunzi wakuya pang’ono wa Iwo; Mzimu Woyera, mwa ubatizo wa Iwo, mthunzi wakuyapo; tsopano Mzimu Woyera, mwa kubwezeretsa kwa Umunthu Wake womwe kukhala uli pano, ukuchita zizindikiro ndi zodabwitsa monga Iye anachitira pa chiyambi. Psyii! Ulemerero! Munditcha ine “woyera-wodzigudubuza,” mulimonse, inu mukhoza kungoyambiratu pano.

<sup>87</sup> Mvetserani, abale, mvetserani kwa ichi.

*...magome onse ali odzaza ndi masanzi...palibe malo oyera.*

*Ndani yemwe iye ati adzamuphunzitse chidziwitso? ...ndani yemwe iye ati adzamupangitse kuti adziwe, kumvetsa chiphunzitso? iwo amene achotsedwa ku mkaka, ndipo atachotsedwa ku maere.*

Osati ana aang’ono; makanda Achipresibateria, makanda Amethodisti, makanda Achipentekoste, makanda Achilutera, makanda Anazerini. Iye akufuna winawake yemwe ali kulolera kuti achoke ku maere ndi kumadya chakudyaya china cholimba. Izi zikubwera apazi:

*Pakuti langizo liyenera kukhala pa langizo, ...pa langizo; mzere pa mzere, ...pa mzere; pano pang’ono, ndi apo pang’ono:*

*Pakuti ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena Ine ndidzayankhula kwa anthu awa.*

*Kwa omwe iye anati, Uwu ndi mpumulo umene inu mungawapangitse otopa kuti apumule; ndipo uku ndiko kutsitsimutsa: komabe iwo samakhoza kumwa.*

<sup>88</sup> Mzimu Woyera, ngati umo siziri basi momwe Iwo unadzera pa Tsiku la Pentekoste, unalosedwa zaka mazana asanu ndi awiri mphambu khumi ndi ziwiri Iwo usanabwere! Pano Iwo uli pa Tsiku la Pentekoste, unabwera chimodzimidzi basi.

<sup>89</sup> Winawake anati, “Kusunga tsiku la sabata.” Ine sindikukana kapena kupanga kuwala kwa mpingo wa wina aliyense kapena chipembedzo. Koma anati, “Tsiku la sabata, sabata ya Mulungu inali tsiku lopuma.”

*Ili ndilo tsiku lopuma. [M’bale Branham akunyamula Baibulo lake.] “Uwu ndiwo mpumulo,” Iye anati, “kuti inu muwapangitse otopa kuti apumule.” Uwu ndi iwo. Ameni! “Iwo udzakhala langizo pa langizo, mzere pa mzere.” Apa pali mpumulo. Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Mpumulo. O!*

*Bwerani kwa ine, nonse inu amene mukuvutika ndipo muli olemedwa kwambiri, ndipo Ine ndidzakupatsani inu mpumulo.*

<sup>90</sup> Kodi Iye ndi chiyani? Mmodzi yemwe amabwera mwa inu, amakupatsani inu mtendere; chizindikiro chanu, Mtonthozi wanu; kutonthozedwa, pa mpumulo, osindikizidwa.

<sup>91</sup> Inu muli bwanji? Iwo ndi chizindikiro; dziko limadziwa kuti chinachake chachitika kwa inu. Kodi Iwo ndi chiyani? Iwo ndi Mtonthozi. Kodi Iwo ndi chiyani? Chisindikizo. Iwe uli pa mpumulo. Iwe uli naye. . . Iwo ndi Woyimira mulandu wanu. Ngati, inu, chinachake chikachitika kwa inu, pali Chinachake pamenepo choti chipange wokuyimirani mulandu inu pomwepo mwamsanga, mwaona, kupanga chitetezero. Ndiwo Mzimu wa Mulungu ukukhala mu Mpingo, unaneneredwa chimodzimodzi chomwe Iwo ukanati ukhale pamene Iwo ubwera. Iwo udzakhala wanthawizonse, mpumulo Wamuyaya.

<sup>92</sup> Mulungu anapanga dziko. Ahebri, mutu wa 4. “Mulungu anapanga dziko, ndipo anapumula pa tsiku lachisanu ndi chiwiri.” Ndiko kulondola.

Tsiku lachisanu ndi chitatu anabwerera mmbuyo mozungulira, pansi. . . Iye apereka icho kwa Ayuda mwa pangano, kwa muyezo winawake wa nthawi. Ndiko kulondola. Koma iwo amapita ndi kukapuma tsiku limodzi; kubwerera mmbuyo, tsiku loyamba la sabata, kuyambira kachiwiri, mwatsopano, kuyambiranso. Umenewo si mpumulo umene Mulungu ankawukamba.

Pamene Mulungu anapanga dziko mu masiku asanu ndi limodzi, pamene Iye anapita kukapuma, Iye anapumula kuchokera pamenepo mpakana. Ndiko kulondola. Icho chinakhazikitsa izo. Iye sanabwerere mmbuyo pa tsiku lachisanu ndi chitatu ndi kuyambira kachiwiri.

<sup>93</sup> Uwo unali mthunzi chabe. Tsopano, icho chinali choyimira, monga mwezi kwa dzuwa; koma pamene dzuwa lituluka, ife sitimausowa mwezi kenanso ayi. Tsopano zindikirani izi, o, mu Chivumbulutso 11, “Mkazi ali ndi mwezi pansi pa mapazi ake, ndipo dzuwa liri pa mutu wake.” O, ife tikanakhoza kupita kudutsa mu Baibulo, kuchokera ku chivinikiro mpaka ku chivinikiro, ndi kukusonyezani inu. Mwaona?

<sup>94</sup> Koma iwo ndi chiyani? Pamene, Baibulo linati mu Ahebri mutu wa 4, “Ngati Yesu akanati awapatse iwo tsiku lopuma, Iye akanati mtsogolo mwake adzayankhule za ilo; Iye akanati adzayankhule za tsiku lopumula.” Ndi tsiku lanji Iye anayankhula za, mpumulo?

*Bwerani kwa ine, nonse inu amene mukuvutika ndipo muli olemedwa kwambiri, ndipo Ine ndidzakupatsani inu mpumulo.*



<sup>95</sup> Mateyu mutu wa 11, ndime ya 22...Penyani, ndiye, ife timawupeza iwo pamene ife tibwera kwa Iye. “Pakuti iye,” anatero Ahebri 4, “yemwe walowa mu mpumulo wa Yesu, watha ku ntchito zake za chidziko, monga Mulungu anachita ku Zake,” pamene Iye anapanga dziko, kuti asati adzabwerere kwa izo kachiwiri. Motalika chotani? [M’bale Branham akugogoda pa guwa katatu—Mkonzi.] Ndi motalika chotani inu muli osindikizidwa nawo Mzimu Woyera? “Kufikirira tsiku la chiwombolo chanu.” Pamenepo pali mpumulo umenewo, chithonhozo, Woyimira mulandu, chisindikizo, Wowombola. O! [M’bale Branham akuwombetsa manja ake palimodzi kamodzi.] Ine ndikukhala ngati ndatengeka, kapena ine ndikukhala ngati ndikudalitsidwa. O!

<sup>96</sup> “Kodi Iwo uli wolonjezedwa kwa ife, M’bale Branham? Kodi izo ziri zotsimikiziridwa ndi Baibulo?”

Chabwino, tiyeni tipite ku Yoweli, tikapeze zimene Yoweli ananena za Iwo.

Momwe ndiriri wothokoza kwambiri chifukwa cha Mawu odala a Mulungu! Kodi inu mukuwakonda Iwo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ine ndikuganiza kuti ngati akanati asakhale Mawu, ine sindikudziwa pamene tikanati tiyime. Chabwino.

Ife tiri pa Yoweli tsopano. Ife tikupita ku Yoweli, mutu wa 2 wa Yoweli, ndipo ife tikuti tiyambire pa ndime ya 28. Yoweli 2:28, zaka mazana asanu ndi atatu kusanafike kudza kwa Khristu, mneneri mu Mzimu. Tsopano mveterani.

*Ndipo izo zidzafika pochitika mtsogolomo, kuti ine ndidzatsanulira mzimu wanga pa matupi onse; . . . ana anu amuna ndi ana akazi adzanenera, anthu achikulire anu adzalota maloto, ndipo anyamata anu adzawona masomphenya:*

*Ndiponso pa antchito anga ndi pa adzakazi anga ine ndidzatsanulirapo mu masiku amenewa . . . kutsanulirapo, mu masiku amenewo, za mzimu wanga.*

*Ndipo ine ndidzasonyeza zodabwitsa mu miyamba mmwamba ndi mu dziko lapansi, magazi, . . . moto, ndi nsanamira za utsi.*

*Dzuwa lidzasandulika kukhala mdima, ndipo mwezi kukhala magazi, pamenepo lalikulu ndi . . . tsiku lowopsya la AMBUYE lisanati labwera.*

*Ndipo izo zidzafika pochitika, kuti aliyense amene ati adzayitane pa dzina la AMBUYE adzawomboledwa:*

<sup>97</sup> Ndicho. . . O! Chiyani? Yoweli! Kodi inu munazindikira? Mu Machitidwe 2, Petro anaitenga ndime yomweyo. Anati, “Inu amuna a Israeli, mverani mawu anga. Awa sali oledzera,” anthu osindikizidwa, othonthozedwa, achilendo, olembedwa chizindikiro awa. “Iwo sali oledzera, monga inu mukuganizira,”

Machitidwe 2, “powona kuti ili ndi ora lachitatu la tsiku. Koma ichi ndi chija chimene chinayankhulidwa ndi Yoweli mneneri, kuti, ‘Izo zidzafika pochitika mu masiku otsiriza kuti Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa matupi onse.’”

<sup>98</sup> Ndi chiyani Icho, kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Chabwino, tsopano tiyeni tizindikire kachiwiri, unalongezedwa kwa okhulupirira, ndicho chimene Iwo uli. Tsopano, Mzimu Woyera uwu, ife tikupeza chimene Iwo uli, miniti yokha. Kodi Iwo walongezedwa kwa ndani? Kwa okhulupirira.

Tsopano tiyeni tipite ku Luka, mutu wa 24 wa Luka, mvetserani chimene Yesu ananena mu Mawu Ake otsiriza Iye asanachoke pa dziko lapansi. Luka mutu wa 24. Ndipo inu amene mukulemba izi apo tsopano, inu mukhoza kulemba izo, ndiye mukaziwerenge izo pamene muti mukakhale ndi nthawi yochulukirapo. Tsopano, Luka 24:49, mvetserani kwa Yesu akuyankhula. Pa mapeto, pamene Iye anali kukwera mmwamba kupita ku Ulemerero, kukwera, pano pali Mawu amene Iye ananena kwa akuphunzira Ake.

. . . taonani, Ine nditumiza lonjezo la Atate anga . . .

Lonjezo lanji? Chisindikizo, chizindikiro, Mtonthozi, ndi zinthu zonse izi zimene ine ndazikamba, kuphatikiza zikwi zinanso.

. . . Ine nditumiza lonjezo la Atate anga pa inu. . .

Lonjezo lanji? “Ilo limene Yesaya anati likanati lidzadze, ‘Ndi milomo yachibwibwi ndi malirime ena ine ndidzayankhula kwa anthu awa.’ Ine ndidzatumiza mpumulo umenewo pa inu. Ine ndidzatumiza chimene Yoweli anachikamba, kuti, ‘Kudzafika pochitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa inu.’ O, ine ndidzatumiza kwa inu, ndi kupanga mafuko onse, anthu onse, kuyambira ku Yerusalemu. . . Ine ndidzabweretsa mkati mbewu ya Abrahamu pansu pa pangano ili. Ine ndidzasindikiza mmodzi aliyense wa iwo. Mwaona, ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga.”

. . . Ine ndidzatumiza lonjezo la Atate anga pa inu:  
koma dikirani inu, kutanthawuza, yembekezerani mu  
mzinda wa Yerusalemu, kufikira muli odzazidwa ndi  
mphamvu yochokera kumwamba.

<sup>99</sup> Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani ndiye? “Mphamvu yochokera Kumwamba!” Osati mphamvu yochokera kwa a bishopu, osati mphamvu yochokera ku mpingo. Koma, “Mphamvu yochokera Kumwamba!”

<sup>100</sup> Kodi mphamvu imeneyo inabwera motani? Mwa “kujowina mpingo”? Ine ndikutsutsani inu kuti mukutero, kunena kuti ndiko kulondola. Mwa “kujowina mpingo, kugwirana chanza ndi mlaliki”? Ayi, bwana. Tsopano, kwa inu Akatolika,

“kutulutsira kunja lirime lanu ndi kutenga mgonero woyamba”? Ayi, bwana.

<sup>101</sup> Kodi Iyo inabwera chotani, Mphamvu yochokera Kumwamba? Tiyeni tiwerenge patsogolo pang’ono. Tiyeni tipite ku Machitidwe 1:8. Iwo akusonkhana palimodzi tsopano. Tsopano iwo anali akuyankhula za Yesu apa, pamene iwo anali atasonkhana palimodzi, ndipo anali atamudzoza mmodzi wina kuti atenge malo a Yudasi. Machitidwe 1:8.

*Koma inu mudzalandira mphamvu, zitachitika kuti Mzimu Woyera uwu wabwera pa inu: . . .*

Chiyani? “Inu mumakhala chiwalo cha Branham Tabernacle”? Ayi. “Iwe umakhala chiwalo cha mpingo wa Methodist, mpingo wa Katolika, Chipresibateria”? Siziri choncho, mu Baibulo. Ndicho chiphunzitso chopangidwa ndi anthu.

“Koma inu mudzalandira Mphamvu inu mutakhala kaye mlaliki?” Ayi, bwana. “Inu mudzalandira Mphamvu inu mutatenga kaye Bachala yanu ya Luso”? Ayi, bwana. “Inu mudza- . . . idzabwera Mphamvu mutapeza kaye DD yanu”? Ayi, bwana. “Inu mudzalandira Mphamvu inu mutabatizidwa kaye mmadzi”? Ayi, bwana. “Inu mudzalandira Mphamvu mutadya kaye mgonero woyamba”? Ayi, bwana. Mwaona, izo zonse ndi zinthu zopangidwa ndi anthu.

<sup>102</sup> Mvetserani chimene Baibulo linanena, chimene Yesu ananena.

*. . . inu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera ukadzabwera kaye pa inu: (kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Mphamvu) ndiye, zitachitika izi, inu mudzakhala mboni. . . (“Inu khumi ndi awiri nokha, inu mboni za ku Yerusalemu”?) . . . inu mudzakhala mboni kwa ine konse mu Yerusalemu, . . . Yudeya, . . . Samaria, ndi ku mbali zakutali za dziko lapansi. (Zomwe sizinayambe zafikidwa panobe.)*

*Ndipo pamene iye anali atayankhula zinthu izi, . . . pamene iye anali atayankhula zinthu izi, pamene iwo ankamuyang’ana iye, iye anatengedwera mmwamba mu mtambo ndipo analandiridwa. . . kuchoka ku kupenya kwawo.*

<sup>103</sup> Tsopano tembenuzirani kwina tsambalo, yang’anani mauneneri awa akufika poti akwaniritsidwe.

*Ndipo pamene tsiku la Pentekoste linali litadza kwathunthu, iwo anali mu umodzi. . . iwo anali onse ndi mtima umodzi mu malo amodzi.*

“Ndipo zonse mwadzidzidzi abusa anabwera mkati ndipo . . .”? Ine ndinachoka pa mzere pamenepo, sichoncho ine? “Zonse mwadzidzidzi wansembe anabwera pa guwa?” Ayi.

*Ndipo mwadzidzidzi apo panadza mkokomo . . .*

Osati chabe kudzipangitsa-kukhulupirira; Iwo unali pamene, mkokomo.

“Mtumiki anali kuyandikira pakhomo”? “Wansembe anali ndi mgonero, akubwera kuchokera ku malo oyera”? Ayi, zonga zimenezo.

*. . . apo panadza mkokomo wochokera kumwamba . . .  
(Osati kukhwakhwaza kwa mapazi) . . . apo panadza  
mkokomo wochokera kumwamba ngati . . . mphepo ya  
mkokomo wamphamvu (o, mai! Whushii! . . . ? . . .) . . .  
ndipo iyo inadzaza nyumba yonse kumene iwo anali  
atakhala.*

<sup>104</sup> Kodi Mzimu Woyera ndi Chiyani? Apa ndi pamene iwo analandirira Mphamvu. Apa ndi pamene iwo ankayenera kuti ayembekezere; pano pali chimene chinachitika pamene iwo anachita izo. Onse analosera, kuchokera ku Genesisi mpaka kupitirira chokwera, kuchokera kwa Abrahamu kupitirira mpaka kupyola; Iwo ukanabwera, ndi momwe Iwo ukanabwera, ndi zotsatira zikanati zibwere. Kodi Iwo ndi chiyani? Zolonjezedwa kwa Mpingo, kwa okhulupirira.

*. . . ndi kudzaza nyumba yonse kumene iwo anali  
atakhala.*

*Ndipo kumeneko anawoneka kwa iwo malirime  
ogawika monga . . . a moto, ndipo iwo anakhala pa  
aliyense wa iwo.*

*Ndipo iwo onse anali atadzazidwa ndi Mzimu Woyera,  
ndipo anayamba kuyankhula ndi malirime ena, pamene  
Mzimu umawapatsa iwo mayankhulidwe.*

Tsopano ife tikuti tidzafike pa zimenezo, Lachisanu usiku. Ife tizisiyira izo apo pomwe, mwaona.

<sup>105</sup> Ziri motani Izo? Ndiwo lonjezo la kwa Mpingo, mwamtheradi lonjezo. Chabwino.

<sup>106</sup> Tsopano, tsopano ife tati tipeze, iwo atadzazidwa kaye, iwo anasindikizidwa kufikira motalika bwanji? [Osonkhana akuti, “Kufikira tsiku la chiwombolo.”—Mkonzi.]

Ndi angati muno ali nawo Mzimu Woyera? Tiyeni tiwone manja anu. Alipo ambiri omwe ali nawo Mzimu Woyera kuposa omwe alipo opanda. Ife tikufuna inu kuti mukhale amodzi a ife, m'bale, mlongo. Pamene inu mumvetsa chimene Iwo uli, Ndiwo . . . Iwo ndi Mzimu wa Mulungu ukukhala mwa inu, kuti uzichita ntchito za Mulungu.

Pamene Mulungu atumiza konse uliwonse wa Mzimu Wake mwa aliyense wa antchito Ake, aliyense wa aneneri Ake, aliyense wa aphunzitsi Ake, aliyense wa atumwi Ake, iwo anali nthawizonse okanidwa ndi dziko. Iwo ankayesedwa openga,

mu m'badwo uliwonse umene iwo analimo. Ngakhale pamene Paulo anayima pamaso pa Agrippa, iye anati, “Mu njira yomwe izo zikutchedwa zosokonezeka. . .” Kodi *chosokonezeka* ndi chiyani? “Kupenga.” “Mu njira yomwe iwo amaitcha zopenga, gulu la zitsiru, ndi momwe ine ndimapembedzera Mulungu wa Makolo athu.” [M'bale Branham akuwombetsa manja ake palimodzi kamodzi—Mkonzi.] Ine ndine wokondwa kwambiri kuti ine ndingakhoze kunena kuti ndine mmodzi wa iwo. Inde, bwana. Ndiko kulondola. Ine ndine wokondwa kwambiri kuti ine ndingakhoze kunena kuti ndine mmodzi wa iwo.

<sup>107</sup> Tsopano, zitachitika izi Mzimu Woyera utagwera pa iwo, Iwo unawapangitsa iwo amitima yokoma kwambiri kufikira chirichonse chinali cha limodzi. Ndi kulondola uko? Mai, mai, ndi chiyanjano bwanji! Ife timayimba nyimbo imeneyo nthawizina, “O, ndi chiyanjano bwanji! O, ndi chisangalalo Chauzimu bwanji!” Ndi chimenecho. Iwo sanali kusamala, iwo sanali kusamala kaya—dzuwa liwala kapena siliwala. Iwo sanali kupempha kama wamaluwa a zofewa.

“Tsopano, ine ndilandira Mzimu Woyera,” amatero anthu ena kwa ine, “Bambo Branham, ngati inu muti mundipatse ine chitsimikizo kuti ine ndikhala wamamilioni, ngati inu muti mundipatse ine chitsimikizo kuti ndipeza zitsime za mafuta, ndipo ine ndipeza migodi ya golide, ndipo ine—ine. . .” Mwaona, anthu amaphunzitsa zimenezo, ndipo iwo amaphunzitsa bodza. Mulungu sanalonjeze zinthu zimenezo.

<sup>108</sup> Munthu yemwe amalandira konse Mzimu Woyera samasamala kaya iye azipempha mkate, kapena ayi. Sizimapanga kusiyana kulikonse kwa iye. Iye ndi cholengedwa chomka-Kumwamba. Iye sasamala. . .Iye alibe zingwe kuno, nkomwe. Ndiko kulondola. Iye samasamala. Siyani zibwere, siyani zipite, kaya chiyani. Asiyeni iwo azitsutsa, kukhala akunyodola. Kutaya kutchuka kwanu, inu mukusamala chiyani? Inu muli pa ulendo wanu waku Ulemerero! Aleluya! Maso anu akhazikika pa Khristu, ndipo inu muli pa msewu wanu. Inu simukusamala chimene dziko likunena.

Ndi chimene Mzimu Woyera uli. Ndiwo Mphamvu, Ndiwo chisindikizo, Ndiwo Mtonthozi, Ndiwo Woyimira mulandu, Ndiwo chizindikiro. O, mai! Ndiwo chitsimikizo chakuti Mulungu wakulandirani inu.

Ndi nthawi yochuluka chotani yomwe ine ndatenga? Ine ndatsala ndi maminiti asanu ndi atatu okha owonjezera. Chabwino. Ndisiyeni ine. . .Ine ndiri nawo Malemba ambiri apa. Ine sindikuganiza ine ndingakhoze kuwatengera iwo mkati, koma ife titi—ife tityesa mwakukhoza kwathu.

<sup>109</sup> Tsopano, munthu atadzazidwa kaye ndi Mzimu Woyera, kodi nkotheke kuti mazunzo ndi zinthu zingati zimupangitse iye kuti abwerere mmbuyo ndi. . .Tsopano, iye sataya, iye akadali

mwana wamwamuna wa Mulungu, iye adzakhala nthawizonse ali, chifukwa iwe wasindikizidwa motalika chotani? [Osonkhana akuti, “Kufikira tsiku la chiwombolo.”—Mkonzi.] Ndiko kulondola. Ndicho chimene Baibulo linanena.

<sup>110</sup> Tsopano, ophunzira atamenyedwa kaye, iwo akhala akusekedwa, kukhala akunyogodoredwa, ndi chirichonse, iwo anaganiza kuti ndi nthawi yoti abwerere mmbuyo palimodzi kwa kanthawi pang’ono. Tiyeni titembenuzire ku—ku Machitidwe mutu wa 4, ndipo tiwone pamene iwo. . . chimene chinachitika. Tsopano izi ndi za kwa inu anthu omwe muli nawo kale Iwo. Machitidwe mutu wa 4.

Tsopano, Petro ndi Yohane anali atamenyedwa kale, kuyikidwa mu ndende, chifukwa cha machiritso, pokhala ndi utumiki wa machiritso kunja pa chipata cha mpingo. Ndi angati akudziwa zimenezo? Apo panali munthu ali pamenepo, wokhala ngati wolumala mu phazi lake. Iye samakhoza kuyenda; anakhala ali motero kwa zaka makumi anayi. Ndipo Petro anadutsa pamenepo. Ndipo iye anati. . . anagwirizitsa chikho chake, kuti alandire chinachake choti ayike mu chikho chake, cha chakudya.

Ndipo Petro anasonyeza kuti iye anali mlaliki wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, iye analibe ndalama iliyonse. Iye anati—iye anati, “Siliva ndi golide ine ndiribe konse.” Mwaona, iye sanali kusamala za zimenezo. Koma iye anali cho—cholengedwa chomka-Kumwamba. O, momwe ine ndikukhumbira tikadakhala ndi nthawi yoti tikhale mu zimenezo mwa kanthawi pang’ono apo, onani. Iye anali womka-Wakumwamba. Iye anali wopeza bwino. Iye anali nawo Mzimu. Iye anali nayo Mphamvu. Iye anayenda mopitiriza ndipo anati, “Siliva ndi golide ine ndiribe konse, koma icho chimene ine ndiri nacho ine ndipereka kwa iwe.”

Mosakaika munthuyo anati, “Inu muli ndi chiyani, bwana?”

“Ine ndiri nacho chikhulupiro. Ine ndiri nacho chinachake mu mtima wanga chimene chinayamba pafupi masiku khumi apitawo. Ine ndinali mu chipinda chapamwamba kumtunda uko, ndipo zonse mwadzidzidzi, malonjezo onse amene Mulungu anawapanga. . . Ine ndinali nditayenda naye Yesu Khristu kwa zaka zitatu ndi theka. Ine ndinkaweza naye Iye, uko tikukoka nsomba. Ine ndachita zinthu zosiyana izi. Ndipo ine ndimamuwona Iye akuwachiza odwala. Ine. . . Iye ankapitiriza kundiwuza ine, ‘Atate ali mwa Ine; koma pamene Ine ndichoka, Iye adzabwera mwa iwe.’ Chotero, ine sindinkakhoza kumvetsa zimenezo. Koma Iye anati, ‘Tsopano, ine sindikuyembekeza kuti inu muzimvetsa izo.’”

Inu simuli kuzimvetsa zinthu izi; inu mukungozitenga izo. Ine sindiri kuzimvetsa izo panobe. Ndipo inu musati mundiuze ine kuti inu mukumvetsa; chifukwa, inu simuli.

Mwaona? Chotero, ine sindingakhoze kuwumvetsa Iwo, ine sindingakhoze kuwufotokoza Iwo; koma, chinthu chokha chimene ine ndikuchidziwa, ine ndiri nawo Iwo.

“Chabwino, chabwino,” inu mukuti, “izo siziri mwasayansi ayi.” O, zedi izo ziri.

<sup>111</sup> Tayang’anani pa magetsi awo. Pamene Benjamin Franklin anawagwira iwo, iye anati, “Ine ndawapeza iwo.” Iye sanali kudziwa chimene iye anali nacho, koma iye anali nawo iwo. Ndipo ine ndikufuna winawake kuti andiwuze ine usikuuno chomwe magetsi ali. Iwo sakudziwa panobe chomwe iwo ali, koma ife tiri nawo iwo. Amen. Ndiko kulondola. Palibe munthu yemwe amadziwa chimene magetsi ali. Iwo akhoza kuwaweta iwo, kuwapangitsa iwo kuyaka, kuwapangitsa iwo kuwotcha, kuwapangitsa iwo kuchita. Koma iwo—iwo amapukusidwa ndi magudumu, zidutswa ziwiri zikuthamanga limodzi moga *choncho*. Izo zimapereka izo, ndipo ndizo zonse zimene iwo akudziwa. Iwo amapereka kuwala, ndipo iwo ali nayo mphamvu mwa iwo.

<sup>112</sup> Ndipo ziri moga Mzimu wa Mulungu. Pamene iwe utenga chidutswa chimodzi, ndicho iweyo, ndipo chidutswa chinacho ndi Mulungu; ndipo ukazifikitsa izo poyenda mozungulira limodzi moga *choncho*, izo zikuchitira chinachake kwa iwe. Ndiko kulondola. Izo zipereka Kuwala. Izo zipereka Mphamvu. Iwe sumadziwa chimene Iwo uli, ndipo iwe sudzadziwa konse chimene Iwo uli, koma iwe umadziwa pamene iwe uwulandira Iwo. Ndicho chinthu chimodzi motsimikiza. Ndipo Iwo ndi wa kwa iwe. Ndi wako. Ndiwo chitsimikizo. Ndiko kulondola.

Kodi kuwala *kumeneko* kumasonyeza chiyani? Apo pali chitsimikizo. Iko ndi kuwala.

Tsopano zindikirani ichi. Tsopano, inu simukudziwa chimene Iwo uli.

<sup>113</sup> Koma anthu awa anati, “Chabwino,” iwo adza. . . iwo anati chinthu chimodzi chimene iwo akuchidziwa, “ife tikudziwa kuti iwo ndi osaphunzira.” “Manati,” enanso inu mukuona, moga Mgermani wamng’ono anati iye anali. Mwaona? Anati, “Iwo ndi mbuli ndi mbuli. Koma iwo akhala ali ndi Nsodzi uja, Kalipentala uja uko kutsidya, wotchedwa Yesu, ine ndikukuuzani inu, chifukwa iwo akuchita zinthu zomwezo zimene Iye amachita.”

<sup>114</sup> Ndicho chimene Mzimu Woyera uli, ndi Yesu akukhala mwa nsodzi wosadziwa, kalipentala, kapena chirichonse, mlaliki wosadziwa, chirichonse chimene icho chiri. Ndi munthu yemwe akufuna kukhala ali wosadziwa ku zinthu za dziko, ndi kumulola Yesu kubwera mwa iye, Mzimu wa Mulungu, chisindikizo, Mtonthozi. Iye sasamala za kutchuka; chinthu chokha chimene iye akuchifuna ndi Mulungu.

<sup>115</sup> Pamene Mulungu anali akuyika mu dongosolo, Iye anati, “Inu nonse Alevi, ine ndakuyitanani inu ndipo ndakupangani inu ansembe. Ndipo abale anu onse, ena, mafuko khumi ndi awiri ndi. . . mafuko ena khumi ndi limodzi azikulipirani inu chachikhumi.”

“Pamene, inu mupeza mitanga isanu ndi inayi ya maapulo, muzitsanulira mtanga umodzi kwa Alevi. Pamene inu muyendetsa nkhosa yanu kudutsa mu ho—holo pano, muzitengapo nkhosa yachikhumi. Ine sindikusamala ngati iyo ili yaying’ono, kapena yayikuluyo, yonenepayo, kapena yonyozekayo, imeneyo ndi ya Mlevi.

“Tsopano, Alevi, pamene inu mupeza zonse izi, ndiye inu muzipereka chachikhumi, inunso, kwa Ambuye. Inu muzipanga chopereka-choweyula, zopereka-zokweza, zopereka zosiyana. Inu muzipereka chachikhumi kwa Ambuye.”

<sup>116</sup> Anati, “Mose, kwa gawo lako, Ine ndine wako.” O, mai! Iye anati, “Ndine gawo lako lokhutitsa.”

Ndipo ndicho chimene Mzimu Woyera uli kwa Mpingo lero. Siliva ndi golide ine ndiribe, koma ine ndiri nalo Gawo lokhutitsa. Aleluya! Maphunziro, ine sindingakhoze konse kuwerenga Bukhu ili, koma ine ndiri nalo Gawo lokhutitsa. Ndizo zabwino. Digirii ya Udokotala, ine ndiribe iliyonse; ma Ph.D kapena ma LD, kapena kanthu kalikonse. Koma pali chinthu chimodzi chimene ine ndiri nacho, Gawo lokhutitsa. Ndilo gawo limene ine ndikulifuna. Ndilo gawo limene Mulungu akufuna kuti inu mukhale nalo. Ponyerani zonse za zinthu zakale izi kutali, kunyada konse ndi china chirichonse, ndipo yenderani kunjani kukapeza Gawo lokhutitsa la Mulungu.

<sup>117</sup> Pakuti, chimene inu muli nacho cha dziko lapansi ili, inu mudzachisiya kuno pamene inu mudzachoka. Koma ngati inu muli nalo Gawo lokhutitsa ilo, Ilo lidzakutengerani inu mmwamba motsimikiza basi. Iye nthawizonse tikumakatenga inshulanse, lero, kuti timupatse woyikitsa maliro. Tiyeni tipeze Gawo lokhutitsa la Mulungu, ndi kupeza Wotitengera Mmwamba mmalo mwa wotiyika pansu. Inu mukudziwa, iwo onse amagwira ntchito.

<sup>118</sup> Tsopano tiyeni tiwone.

*. . . ataloledwa kuti apite, iwo anapita kwa oyanjana nawo awo, . . .*

Osati kubwerera kwa ansembe. Mwaona, izo zinasonyeza kuti iwo anali nawo Iwo. Iwo sanali kubwerera ku chinthu chakale, chozizira, chamawonekedwe chija kachiwiri, ayi; kubwerera kumbuyo ndi kukati, “Tsopano taonani apa chimene iwo anachita kwa ife!” Ayi, ayi. Iwo anali nawo oyanjana nawo awo. Uko kunali pafupi dazeni lokha la iwo kumeneko, koma amenewo anali oyanjana nawo okwanira, anthu owerengeka pang’ono ongokwanira mdzanja.



*... atawalola kuti apite, ...*

Atatha kuwakwapula iwo ndi kuwawopsyeza iwo, anati, “Ngati inu muti mudzabatize konse mu Dzina la Yesu kachiwiri!” Kapena, o, ine ndimatanthauza... Chabwino, uko nkulondola. Mukuona? “Ngati inu muti mudzabatize konse mu Dzina la Yesu kachiwiri, chirichonse chimene inu mumachita, ife tidzakupezani inu!”

<sup>119</sup> Anati, “Psyii, uko nkuwopsyeza ndithu. Tiyeni tipite kwa abale ena onse.” O, ndiko kachitidwe. Mu umodzi muli mphamvu. Mu umodzi muli mphamvu. Anati, “Tiyeni tingopita kwa ena onse a abale ndi kukapeza chimene ife tikanakhoza kuchichita.”

<sup>120</sup> Tsopano iwo onse anabwera palimodzi ndipo anali akunena zowachitikira zosiyana.

*... ataloledwa kuti apite, iwo anapita kwa oyanjana nawo awo, ndipo anakafotokoza zonse zimene wansembe wamkulu ndi aakulu anali atanena kwa iwo.*

*Ndipo pamene iwo anali atamva izo, iwo anakweza maliwu awo kwa Mulungu ndi mtima umodzi, ...*

Tsopano mverani chimene iwo ananena. Mpenyeni iye, apenyeni iwo, osati kubwereramo ndi kukati, o, chinthu china chimzake chakuti, “O Ambuye, ine ndikupepesa...” Ayi. Iwo anali atapulumsidwa kale. Iwo anali atadzazidwa nawo Mzimu. Iwo anali nawo Moyo Wamuyaya.

*... anakweza mmwamba maliwu awo... ndi mtima umodzi, ndipo anati, Ambuye, inu ndinu Mulungu, ...*

Ameni! Ine ndimangokonda zimenezo, M’bale Palmer. Ine ndimakonda zimenezo.

*... inu ndinu Mulungu (ife tikudziwa zimenezo) yemwe munapanga miyamba, ndi dziko lapansi, ndi nyanja, ndi zonse zomwe ziri momwemo:*

*Yemwe mwa kamwa ya wantchito wanu Davide... munati, ...*

<sup>121</sup> Tsopano penyani, inu mubwerera mmbuyo, kuti, “Tsopano, ife sindife...” Tsopano inu mumapita kunja uko ndi kumati, “Chabwino, tsopano, Ambuye, tsopano dikirani miniti pano. Iwo akhala akunyogodola kochuluka za ine!” Kodi Iye sanati iwo adzachita izo?

“Onse amene amakhala mwaumulungu mwa Khristu Yesu adzamva kuwawa mazunzo.”

“Chabwino, inu mukudziwa, bwana anga anandiuza ine ngati iye ati andigwire...” Kodi sananene kuti iwo adzanena zimenezo? “Chabwino, inu mukudziwa, iwo ananditengera ine mu bwalo lamilandu tsiku lina, pokhudza Izo.”

<sup>122</sup> Kodi Iye sanati, “Inu mudzatengeredwa pamaso pa mafumu ndi olamulira, chifukwa cha Dzina Langa. Musati mulingalire zomwe muti mukanene, chifukwa sindinu amene mukuyankhula”? Ine ndinawona izo zikuchitika dzulo. “Ndi Mzimu Woyera umene umakhala mwa inu; Iye adzachita kuyankhulako.” Mwaona, “Iye.” Ndiko kulondola. Chabwino. “Musati muganizire zomwe muti mukanene.”

Ambuye, mwa... *Yemwe mwa wanu... kamwa ya wantchito wanu Davide anati, Nchifukwa chiyani achikunja anakwiya, ndipo anthuwo analingalira chinthu chachabe?*

*Mafumu a dziko lapansi anayimirira, ndipo olamulira ... anasonkhana palimodzi motsutsa Ambuye, ndi motsutsa Khristu wake.*

*... mwa choonadi, Ambuye, motsutsa mwana wanu woyera Yesu, yemwe inu mwamudzoza, onse Herode, ndi Pontiasi Pilato, ndi Amitundu, ndi anthu a Israeli, ... anasonkhana palimodzi,*

*Kuti achite chirichonse chimene dzanja lanu ndi uphungu wanu walinga kale kuti chichitidwe.*

O, mai! Ine ndikukonda apo. “Ambuye, iwo akungochita chinthu chomwecho chimene Inu munati iwo adzachichita.” Kodi Baibulo linati chiyani?

*Mu masiku otsiriza, pamenepo kudzabwera onyoza, ammutu, odzikuza, okonda zokondweretsa moposa kukonda Mulungu;*

*... okuswa chipangano, overuza mwabodza, amwano, ... onyoza iwo amene ali abwino,*

*Okhala nawo mawonekedwe a umulungu, koma kukana...*

Iwo sanapite konse pamwamba apo ndi kukalandira Mphamvu, “Mzimu Woyera uwu utadza kaye pa inu.”

*Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kukana mphamvu yake: kuchokera kwa oterowo patukani.*

Ndicho chimene Mzimu Woyera uli. Mwaona?

*... chimene walinga... kuti chichitidwe.*

*... tsopano, Ambuye, taonani kuwopsyeza kwawo: ndi—ndipo perekani kwa antchito anu, kuti ndi kulimbamtima konse ife tikhoze kumayankhula mawu anu,*

O, ine ndikukonda zimenezo! Ikani kumbali fupa lakukhumba ilo, ndipo ikani nsana weniweni mmenemo. Tsopano penyani apa.

*... ife tikhoze kumayankhula mawu anu,*

*Mwa kutambasula pamenepo dzanja lanu kuti muzichiritsa;...*

O, m'bale! Ziwanda sikuti zimafa, koma Mzimu Woyera sumafa nawonso. Mwaona?

*...kutambasula pamenepo dzanja lanu kuti muzichiritsa;...kuti zizindikiro ndi zodabwitsa zikhoze kukhala zikuchitidwa mwa dzina la mwana wanu woyera Yesu.*

Inu mukuona zimene iwo anali kukanganirana, sichoncho inu? Iwo akuchita chinthu chomwecho lero, koma izo sizikuchita ubwino uliwonse.

*Ndipo pamene iwo anapemphera, malowo anagwedezeka pamene iwo anasonkhana palimodzi; ndipo iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo ...anayankhula mawu a Mulungu ndi kulimbamtima.*

<sup>123</sup> Psyii! Mai! Iwo anapeza chinachake pamene iwo anapita pamwamba apo, sichoncho iwo? Lonjezo linati ndicho chimene Mzimu Woyera uli, kuti ukupatseni inu kulimbamtima, kuti ukupatseni inu chithonhozo, kuti ukusindikizeni inu, kukupatsani inu chizindikiro. O, mai!

<sup>124</sup> Mvetserani. O, ndikukhumba ife tikanangokhala nayo nthawi, ife tikanakhoza kukafika kumusi ndi Filipo kwa Asamariya. Mu Machitidwe 8:14; inu nonse amene mukulemba izo. Iwo anali atalandira chisangalalo chachikulu, iwo anali ndi machiritso aakulu, koma iwo anali atabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Koma iwo anatumiza ku Yerusalemu, kuti akamutenge Petro; iye anabwera kumeneko ndi kuyika manja pa iwo, ndipo iwo analandira Mzimu Woyera. Machitidwe 8:14.

<sup>125</sup> Amitundu, analipo mmodzi dzina lake Korneliyo. Iye anali munthu wodabwitsa, ankapereka zachikhumi, ankamangira masunagoge kwa anthu, ankalemekeza Mulungu, ankawopa Mulungu; munthu wabwino, Mpresbateria wabwino, Mmethodisti, Mbaptisti, kapena chinachake chimzake, mwaona, munthu wabwino kwambiri. Koma tsiku lina, Mulungu anati, "Iye ndi munthu wabwino; kotero ine ndingomutumiza iye ku msonkhano. Ine ndiyenera kuti ndimubweretse mlaliki wanga kuno ndi kudzamuwuza iye za Iwo." Chabwino.

Kotero iye anawona masomphenya, anati, "Pita uko ku Yoppa, ndipo iwe ukampeza mmodzi kumeneko dzina lake Simoni, wofufuta zikopa. Ndipo kumeneko kuli mmodzi, Simoni Petro, mmenemo. Mulole iye abwere kuno; iye adzakuwuza iwe njira, chifukwa iye walandira chinachake."

<sup>126</sup> Ndipo pamene Petro anayimirira pamenepo...Ndipo Korneliyo ankafuna kuti amupembedze mlaliki ameneyo. Iye

anali. Koma Petro anati, “Imirira. Ine ndine munthu monga iwe uliri.”

“Ndipo pamene Petro anali chiyankhulire Mawu amenewa,” a momwe iwo anabwererera, mu chiyambi ku... Zinthu zomwezi zimene ine ndikuzikamba, momwe Mulungu analonjezera kudzatsanulira Mzimu Woyera. “Pamene iye anali chiyankhulire Mawu awa, Mzimu Woyera unagwera pa iwo.” Fyuu! Eya. Ndicho chimene Mzimu Woyera uli, womwe Uli wao. Zedi. “Ndipo iwo onse anadzazidwa nawo Mzimu Woyera.”

<sup>127</sup> Tsopano zindikirani mu Aefeso, uko kunali m’bale wa Baptisti. Iye poyamba anali wazamalamulo, wophunzira, munthu waluntha, ankadziwa lamulo; munthu wamkulu, sikolala. Tsiku lina iye anayamba kuwerenga Baibulo, ndipo iye anawona kuti padzabwera mmodzi dzina lake Mesiya. Ndipo pamene iye anachita izo, bwanji, iye anayamba kumva za Yesu uyu, ndipo iye anati, “Ine ndakhutitsidwa. Ndipo ine ndikuvomereza chikhulupiriro changa poyera kuti Yesu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu.” Iye anali Mbatisti weniweni. Apa iye anabwera motsatira, “Ine ndikuvomereza poyera kuti Yesu ndi Khristu.” Iye anayamba kuchita izo mochulukwa kwambiri mwakuti Mulungu anamuyitanira iye ku utumiki. Mulungu nthawizonse adzayankhula kwa mtima wona.

<sup>128</sup> Ndipo kumeneko kunali wopanga mahema wachikulire pang’ono kumusi uko dzina lake Akwila ndi Prisila, mwamuna ndi mkazake. Iwo anali opanga mahema. Machitidwe mutu wa 18, amakuuzani inu za zimenezo. Paulo, iwo anali abwenzi a iye. Iwo anali atalandira Mzimu Woyera pansi pa manja a Paulo ndi kuphunzitsa kwake.

Iwo anamva kuti uko kunali chitsitsimutso uko, chotero iwo anapita kumeneko. Uko kunali pafupi khumi okha kapena khumi ndi awiri ali pamenepo. Kotero iye anapita kumeneko kuti akayang’ane pa icho, ndipo iye anamumva mlaliki uyu akulalikira, mwakudzipereka kwa mtima wake. Iye anati, “Inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira iye angakhoze kumvetsera ku Choonadi.”

Kotero utatha msonkhano, amuyitanira iye kuzungulira kuseri kwa hema, ndipo iye anati, “Penyani, ife tiri naye m’bale wamng’ono wapafupi utali chotere, Myuda wa mphuno-yokhota yaing’ono, ndipo, koma pamene iye abwera kuno, iye adzakuphunzitsani inu Mawu a Mulungu, momveka.” Chabwino, patapita kanthawi. . .

<sup>129</sup> Paulo anali mu ndende pa nthawi yomweyo. Malo oyipa kwa mlaliki wamakono, sichoncho izo? Koma iye anali mu ndende, ndipo Ambuye anali naye iye mmenemo. Kotero chitachitika chivomezi, chinagwedezera ndendeyo pansi, iye anamutenga woyang’anira ndende ndi apabanja lake ndipo anawabatiza iwo

onse, mu Dzina la Ambuye Yesu, ndipo anachokako, anabwera mpaka kumeneko.

Ndipo iye anali atangotulutsa kumene mdierekezi kuchokera mwa wamng'ono, msungwana wamkulu kumeneko wofotokoza zamwayi. Ndipo, ndiye, iwo ali kupanga ndalama zambiri ndi iye, kotero iye anangoyalutsa katangale waoyo, kotero ndiye iwo anamuyika iye mu ndende chifukwa cha icho. Ndipo Ambuye anagwedezera ndendeyo pansi, chifukwa iye anali ndi gulu la anthu cha kumeneko oti amve Choonadi. Inu simungakhoze kuwamanga Mawu a Mulungu. Palibe. . . Ziribe kanthu chiyani, inu simungakhoze. Inu simungakhoze basi kuchita zimenezo.

<sup>130</sup> Kotero iye anabwera mpaka kumeneko kumene munthu uyu anali. Ndipo Akwila ndi Prisila, mwinamwake iwo anali ndi zitumbuwa zina. Ndipo mwamsanga kumene atatha kudya zitumbuwazo, anati, “Ife tipita nawo ku chitsitsimutso.”

Paulo anakhala mmbuyo kumeneko ndipo anagwirizira mwinjiro wake waung'ono, ndipo ankamvetsera kwa mlaliki wa Chibatisti akulalikira.

Iye anati, “Izo ndi zabwino, zimene iwe ukulalikira, koma ziripo zina zowonjezera pa Izo.” Anati, “Ine ndikufuna ndikufunsemi inu funso, Dr. Apollo. Kodi inu mwalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?”

“O,” iye anati, “ife sitimadziwa kuti iwo unalipo. Inu mukutanthauza chiyani, ndi ‘Mzimu Woyera’? Ndife Abaptisti.”

Anati, “Inu mukudziwa bwanji kuti ndinu Abaptisti?” Mwaona?

“Chabwino, ife tinabatizidwa. Ife tikudziwa ubatizo wa Yohane wokha.”

Iye anati, “Iye ankabatiza kokha kulozera ku kulapa, kumanena kuti ‘akhulupirire pa Iye wakudza,’ ndipo pa Yesu Khristu.”

Ndipo pamene iye anamva izi, iwo anabatizidwa kachiwiri, mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo Paulo anasanjika manja ake pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo, ndipo iwo anayankhula mu malirime ndipo analosera. Anati, “aliyense,” tsopano.

<sup>131</sup> Tsopano ife tizichita motani izo? Ine ndikufuna ndikuuzeni inu chinachake, ndiye ine. . . Ife titseka, chifukwa, ndizo, ine ndinakuuzani inu kuti ine ndikutulutsani inu mwamsanga. Inu mukudziwa chimene Mzimu Woyera uli. Kwa Lemba lotsiriza la usikuuno. . . Ine ndiri nawo mulu wina pansi apa, koma ife tichita kuzidumphira zimenezo. Tiyeni titembenezire ku Akorinto Woyamba 12. Ndiyeno ife tiwerenga izi, ndiyeno ife ti—titseka. Chabwino. Akorinto Woyamba, mutu wa 12.

Ndi angati amakhulupirira kuphunzitsa kwa Paulo Woyera? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Zedi! Iye anati, mu

Agalatia 1:8, “Ngati Mngelo aphunzitsa chirichonse chosiyana, musiyeni iye akhale wotembereredwa,” ndiye akati mlaliki. “Ngati Mngelo wochokera Kumwamba abwera pansi ndi kudzaphunzitsa chirichonse chosiyana, musiyeni iye akhale wotembereredwa.” Mwaona, musati mukhale nacho chirichonse chochita ndi izo.

<sup>132</sup> Tsopano penyani izi, Akorinto Woyamba 12. Ndi—ndi angati akudziwa kuti ife tiyenera kuti tikhale mwa Khristu polinga kuti tipite mu chiwukitsiro, chifukwa ndilo Thupi Lake limene Mulungu analilonjeza kuti adzaliwukitsa? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Palibe njira ina. Palibepo njira ina, ngati inu muli kunjira kwa Khristu.

Inu mukhoza kuyang’ana mmbuyo *kuno* ndi kukhulupirira pa Iye, kuti, “Zedi, ine ndikumukhulupirira Iye. Iye ndi Mwana wa Mulungu.” Zabwino, m’bale wanga, ine ndiri wokonzeka kugwira dzanja lanu pamene inu munena zimenezo. “Ine ndikumukhulupirira pa Iye. Ine ndikumuvomereza Iye monga Mpulumutsi wanga.” Ndizo zabwino, koma inu apabe simuli mwa Iye. “Ine ndikugwirana chanza ndi mlaliki. Ine ndikumuvomereza machimo anga.” Zimenezo apabe siziri mwa Iye.

<sup>133</sup> Tsopano penyani, onani zimene Paulo ananena, momwe iwe umalowera mwa Khristu. Kodi iwe udziwidwa motani monga mdulidwe? Abrahamu, iwo ankapereka chizindikiro. Mvetserani ku izi tsopano. Akorinto Woyamba, mutu wa 12, ndipo tiyeni tiyambire pa ndime ya 12.

*Pakuti monga thupi liri limodzi, ndipo liri nazo ziwalo zambiri, ndipo zonse...ziwalo za thupi limodzi limenelo, pokhala zambiri, ziri thupi limodzi: kotero chomwechonso ali Khristu. (Osati ogawanika. “Mmodzi!”)*

Mvetserani. “Pakuti ndi mpingo umodzi”? Ndi angati akuwerenga mmbuyo mwanga? “Mwa kugwirana chanza kumodzi”? “Mwa madzi amodzi”? Ayi. Uyo ndi winawake akulakwitsa.

“Mwa Mzimu umodzi!” Kodi ndi lemba lalikululu? Ndiwo, “Mzimu Woyera,” ndiye. Mwaona?

*...mwa Mzimu umodzi ife tonse tiri obatizidwa kulowa mu thupi limodzi, ngakhale ife tiri Ayuda kapena Amitundu, kaya ife ndife amsinga kapena afulu; ndipo tapangidwa tonse kuti tizimwera mu Mzimu umodzi.*

<sup>134</sup> Thupi la Khristu liri Mzimu umodzi, kumene chiwalo chirichonse, kuchokera ku Pentekoste kufika nthawi ino, akumwa za Vinyo watsopano yemweyo, Mzimu Woyera womwewo, kubweretsa apo zotsatira zofanana. Ife timachita motani izo? “Mwa Mzimu umodzi.”

Ndilo khomo lotseguka la Mulungu, Mzimu Woyera. Ndi chiyani Iwo? Ndiwo khomo lotseguka la Mulungu. Ndiwo chizindikiro. Ndiwo chisindikizo. Ndiwo Chitonthozo. Ndiwo Wotiyimira mulandu. Ndiwo chitsimikizo. Ndiwo mpumulo. Ndiwo mtendere. Ndiwo ubwino. Ndiwo machiritso. Ndiwo Moyo. Ndiwo—Ndiwo khomo lotseguka la Mulungu ku zinthu zonse izi. Ndiwo khomo la Mulungu lotsegukira kwa Khristu, lomwe liri . . .

Mulungu anatsimikizira kuti Iye anamuwukitsa Yesu kuchokera kwa akufa, ndipo iwo amene ali akufa mwa Khristu Mulungu adzawabweretsa ndi Iye pa chiwukitsiro. “Musati muukwiyitse Mzimu Woyera umene mwasindikizidwa nawo kulowa mwa Khristu kufikira tsiku la chiwombolo chanu.” Fyuu! Ndi angati akukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>135</sup> Kodi Khristu ndi chiyani? Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Si chinachake chimene anthu amachiseka. Ndi chinachake chimene anthu amachiseka; koma izo siziri kwa wokhulupirira.

Kwa wosakhulupirira! Ine ndikukhumba ine ndikanakhala nawo masabata awiri kapena atatu aatali, ine ndikufuna ndidzatenge mawa usiku ndi kukuuzani inu chomwe Iwo uli kwa wosakhulupirira. Ndiroleni inu ndingodutsamo, mphindi chabe ya nthawi. Ndiwo chinthu chosekedwa. Ndiwo msampha. Ndiwo chinthu chopunthwitsa. Ndiwo imfa. Ndiko kusiyana Kwamuyaya kuchoka kwa Mulungu. Ine sindingakhoze basi kulingalira za zinthu zomwe Iwo uli kwa wosakhulupirira!

<sup>136</sup> Kumbukirani, mvula yomweyo yomwe wosakhulupirira anali kumayiseka, inali mvula yomweyo yomwe inamupulumutsa Nowa ndi banja lake. Mwaona? Mzimu womwewo, Mzimu Woyera umene anthu ali kumawuseka ndi kunena kuti ndi “misala, ndi gulu la manati, Ndi misala,” Ndi chinthu chomwecho chimene chiti Chidzawukwatule Mpingo ndi kuwutengera Iwo mmwamba pa masiku otsiriza; udzabweretsa chiweruzo pa wosakhulupirira. Ndiko kulondola. Ndicho chimene Mzimu Woyera uli.

<sup>137</sup> Odala ali iwo...Mundirole ine ndinene izi, mwa kudzipereka kwa mtima wanga. Odala ali iwo amene akuchita njala ndi ludzu chifukwa cha Iwo, pakuti iwo adzakhutitsidwa.

<sup>138</sup> Mawa usiku ife tikuti tidzayankhule za momwe, chimene Iwo umachita pamene Iwo ubwera.

<sup>139</sup> Tsopano, ndi angati muno akanafuna kuti alandire Mzimu Woyera, ndipo akufuna winawake kuti akupempherereni inu, kuti inu mudzawone Kuwala?

Inu mukudziwa “chimene Iwo uli.”

Tsopano, mawa usiku, ife tikuti tidzatenge, “chimene Iwo umachita.”

<sup>140</sup> Ndiyeno usiku wotsatira, ndi, “momwe ungawulandirire Iwo.” Ndiye ife tidzayitanira mkati, kukhala ndi anthu pano kulangizidwa, ndi kupita mu zipinda momwe ndi kukakhala mmenemo, ngati izo zititengera tonse kupyola Khrisimasi, ndizo zabwino, kufikira Mzimu Woyera utabwera. Ife tikuti tifike pa Iwo mwa ubwino, maziko a Baibulo. Ife tikuti tifike pa Iwo ndi kuwutenga Iwo basi momwe Mulungu analonjezera Iwo, ndi momwe Iwo unagwera pachiyambi. Ndimo momwe ife tiriri pano kuti tichite izo. Ine . . . Izo sizipanga kusiyana kulikonse chimene chinthu chirichonse chinena, ndife . . .

Mawu a Mulungu ali . . . ali ndi kutsogolera mu mtima wanga. Ndiko kulondola. Ndipo ine ndikufuna chimene Mulungu ali nacho kwa ine. Ngati chiripo chirichonse chowonjezera, Kumwamba kotseguka, Ambuye, chifukwa wanga—mtima wanga ndi wotsegukira kwa izo. Ndiko kulondola.

<sup>141</sup> Ndi angati akuwufuna Iwo? Tsopano kwezani dzanja lanu, itini, “Ndipempherereni ine.” Tsopano, pamene inu mudakali, ndi manja anu mmwamba.

Atate Akumwamba, ife taphunzitsa nthawi yayitali. Koma Mzimu Wanu uli pano. Apo pali manja omwe akwezedwa mmwamba mu malere tsopano. Ndipo iwo akudziwa chimene Iwo uli, iwo akudziwa chimene Mzimu Woyera ukutanthauza. Ine ndikupemphera, Mulungu kuti msonkhano uwu usanathe, kuti dzanja lililonse mkati muno lidzakwezedwa kuti iwo awulandira Iwo. Perekani izo, Ambuye.

<sup>142</sup> Ife tikuwapempherera iwo. Ife tikukupemphani Inu kuti muwadalitse iwo, ndi kuti muwapatse iwo chokhumba cha mtima wao. Yang’anani pa manja awo, Ambuye. Iwo amakukondani Inu. Iwo akuwufuna Iwo. Iwo akudziwa kuti iwo sangakhoze kupita . . . Mawa usiku, ngati muti mundithandize ine, Ambuye, ife tikhoza kutsimikizira izo mu Lemba kuti iwo sadzakhoza kupita mu Mkwatulo popanda Iwo. Kotero ine ndikupemphera, Atate, kuti Inu mukawapatse iwo njala ndi ludzu, kotero kuti iwo akakhoze kukhutitsidwa. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu tsopano, Atate. Ndipo, perekani madalitso awa, pamene ife tikupempha izo mu Dzina la Yesu. Amen.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye  
Poti Iye anayamba kundikonda  
Nagula chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

<sup>143</sup> Ine ndikufuna ndinene izi ife tisanati tiyimbe kachiwiri. Ine ndikufuna kukomana ndi gulu la azitumiki mu chipinda kuno, Lachisanu usiku, msonkhano usanayambe, mwaona, Lachisanu usiku. Ine . . .



Inu mukuona chimene ine ndikuyesa kuchichita? Kuti ndisonyeze chimene Iwo uli, momwe ungafikire pa Iwo ndi choti uchilemekeze; ndiye inu simuli kubwera mwakhungu, kumenya mu chinachake. Ndicho chifukwa ine sindinazipemphe izo usikuuno. Ine ndikufuna inu mudziwe chimene Iwo uli. Ndi lonjezo. Ndiwo chisindikizo. Ndicho Mtonthozi. Ndiwo zina zotero.

Ndiye, mawa usiku ndi usiku wotsatira, ndiye ife tidzayamba apo pomwe, kuchokera apo kupitirira, mpaka Iwo utadza. Sitisamala motalika bwanji momwe izo ziti zitengere; ife tikhala mpakana. Tsukani mtima wanu. Iye sadzawutsanulira konse Iwo mu mtima wosayera. Dzikhaliitsemi bwino, khalani okonzeka, ndipo Iye adzazipereka izo.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye (tiyeni tikweze  
manja athu mmwamba tsopano)  
Poti Iye anayamba kundikonda  
Nagula chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

Abusa angonena kumene, ndipo ife tavomerezana, kuti mawa usiku ife tidzayamba pa seveni mmalo mwa hafu pasiti seveni. Ndipo izo zidzakulolani inu kutuluka pofika hafu pasiti eyiti mmalo mwa hafu pasiti naini. Pa seveni thek-...Pa seveni koloko, mawa usiku, utumiki wa nyimbo udzayamba. Ine ndidzakhala pa Uthenga wanga pa hafu pasiti seveni.

Ndimkonda Iye,  
Tiyeni titulutse mipango yathu ndi kuikupizira kwa Iye.  
Ndimkonda Iye  
Ingoswani kachitidwe kamawonekedweko tsopano!  
Poti Iye anayamba kundikonda  
Nagula chipulumutso changa  
Pa mtengo wa Kalvare.

Chabwino, abusa anu tsopano, M'bale Neville.



*Kodi Mzimu Woyera Ndi Chiyani?*

*(What Is The Holy Ghost?)*

Disembala 16, 1959, Lachitatu usiku

*Kodi Mzimu Woyera Unaperekedwera Chiyani?*

*(What Was The Holy Ghost Given For?)*

Disembala 17, 1959, Lachinayi usiku

Mauthenga awa a William Marrion Branham analalikidwa mu Chingerezi ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A. Kuyesa kulikonse kwachitidwa kuti timasulire molondola Mauthenga oyankhulidwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito kuti adindidwe pa tsamba, ndipo adindidwa ndi kugawidwa mopanda kugulitsa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©1997 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE

P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS

P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)